

TIYENI TIMUWONE MULUNGU



Khalani pansi. Ine ndikupepesa kuti ndachita zimenezo, M'bale Borders, koma panali vuto ladzidzidzi kunja uko, amafa ndi khansa, ndipo ine ndimangoyenera kuti ndipite kumeneko. Basi... Ine ndikudziwa inu mundikhululukira ine chifukwa cha izo. Chotero, izo ziri bwino. Ine ndinadana nazo kuti ndachedwa. Ine ndinali ndikudikirira kwa kanthawi pang'ono chabe, ndipo ndimakumana ndi azimzanga ena, ndipo kenako ine ndinadzabwera ku vuto ili limene linangobweretsedwamo, zoyipa, zoyipa kwambiri, chotero ine ndimayenera kuti ndikafike kwa ilo mwamsanga.

² Ine sindikudziwa kuti ndiyambe bwanji, masana ano. Ine ndimaganizira ndiri pa msewu ndikubwera kuno, “Kodi ndikanene chiyani kwa a—gulu la anthu ngati ili?” Uwu wakhala msonkhano wapamwamba kwambiri kwa ine. Ndipo ine sindikungonena zimenezo basi chifukwa chakuti ndiri patsogolo panu. Ine ndikunena izo chifukwa izo zikuchokera mu mtima mwanga. Ndipo ine ndikufuna kuti aliyense wa atumiki awa adziwe kuti ine ndikuutenga uwu kukhala umodzi wa misonkhano yanga yaikulu imene ine ndinayamba ndakhalapo nayo. Uko nkulondola. Chifukwa cha mgwirizano wanu wabwino ndi chifukwa chake izi zapambana. Ine ndawonapo nthawi zimene pamene panali... Ine ndakhalapo nawo ochuluka mwa omvetsera, anthu ochuluka, koma ine sindinayambe ndawonapo msonkhano umene ine ndinayamba ndakhalapo nawo mmoyo mwanga wa chiyanjano chokoma woposa umene ine ndakhala nawo pakati pa inu abale. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikudalira kuti mipingo yanu ikakula ndi kuwonjezereka mpaka osakhalanso ndi mathero kwa izo. Ine ndikupemphera kuti Mulungu akusungeni inu mu utumiki mpaka Iye adzabwere. Ili ndiro pemphero langa loonamtima la kwa inu. Ndipo ine—ine ndakhalapo ngakhale pamene ine ndinakhalapo ndi atumiki ochuluka mu mgwirizano, monga nthawizina ku Afrika, India, monga choncho, pamene ife timakhala ndi mahandiredi angapo pa boardi. Koma sindinakhalepo ndi nthawi ngati iyi, zochita kuwoneka, kumbuyo kwangaku, mtima umodzi ndi mgwirizano umodzi. Izo ndi zopambana kwenikweni. Ine ndikuyamikira izi, abale. Ndipo ine ndithudi, chirichonse chimene ine ndingati ndikuchitireni inu, mungokumbukira ndine m'bale wanu. Mausiku sadzakhala a mdima kwambiri, mvula siidzagwa kwambiri, mwaona, ine ndidzachita chirichonse chimene ine ndingathe kuti ndikuthandizeni inu kupititsa patsogolo Uthenga waukulu uwu kapena kukuchitirani inu chinachake. Mulungu adzikhala nanu nthawizonse!

³ Ine ndikufuna kuti ndinenenso, kwa m'bale wanga wamng'ono apa, Roy Borders, ine ndangomudziwa kumene M'bale Borders kwa nthawi yochepa. Ine nthawizonse ndakhala ndikufuna nditamupeza winawake amene angamandikonzere ine misonkhano. M'bale Roy akuwoneka kuti wangogunda pa malowo. Iye si mtumiki. Iye ndi mwamuna wamalonda. Ine ndamulolapo iye kukonza misonkhano iwiri kapena itatu, kuti ndingowona chimene iye angachite, ndipo zotsatira zake ndi zimenezi: mgwirizano umodzi. Ndipo kawirikawiri ngati mtumiki abwera kuti adzakukonzere iwe misonkhano, chabwino, nthawizonse pamakhala kuti mtumiki amakhala ndi chinachakenso, ndipo iye amakhala ndi chiphunzitso kapena—kapena chinachake chimzake—chimene iye amafuna kuti achipereke. Ndipo iye amafika pakati pa gulu la atumiki ndipo iye amakapereka chiphunzitso, zikatero—zikatero iwe umakhala mmavuto. Mukuona? Chotero, izo zimakhala zabwino kwa munthu yemwe si mtumiki.

⁴ Tiri pomwepo, ndikubwera, winawake anandifunsa ine, anati, “M'bale Branham, kodi inu ndi wa Yesu Yekha, ndinu wa Yesu Yekha?”

⁵ Ine ndinati, “Mwamtheradi ayi.”

⁶ Ndipo anati, “Winawake anati inu simumakhulupirira mu kuyankhula mmalirime.”

⁷ Ine ndinati, “Iwo samandidziwa ine bwino bwino, ndizo zonse. Ndithudi, ine ndimatero.”

⁸ Tsopano, ndipo M'bale Borders ndithudi ndi njonda ya Chikhristu, wachita ntchito yabwino kwenikweni. Ndipo ine ndithudi ndikumuthokoza M'bale Borders chifukwa chondiyitana ine. Iye wakhala ndi chisoni chochuluka, mavuto ochuluka, koma iye wa—iye wachita ntchito yabwino. Mulungu amudalitse M'bale Borders, ndiro pemphero langa loonamtima.

⁹ M'bale Wagner, ine ndikuganiza iye ali ngati wapampando, ine ndikukhulupirira. Iye ndi amene ine ndakhala ndikukumana naye nthawizonse, wa gululo. Ntchito yapamwamba, chimodzimodzi basi monga anachitira nthawi ina, zabwino. Iye anandiitanira ine kwawo kuti ndikakhale naye, kukakhala mnyumba yake. Ine ndithudi ndikanafuna kuti ndichite zimenezo kwambiri, ine ndimatsala pang'ono kumverera izo. Ine ndinayenera kukana izo chifukwa ine ndinaganiza mwinamwake, ndi chiyanjano chopambana ichi, ine ndingafune kubwera ku nyumba ya wina aliyense, mwaona, kufuna kudzakuwonani aliyense wa inu. Ndipo ine—ine ndinalemekeza kumverera kwanu, ndipo ine ndikutsimikiza M'bale Wagner anamvetsa basi mmene izo zinakhalira, inu mwaona. Kutu ine . . . ngati ine ndingapite kwa M'bale Wagner, ine ndingafune kuti ndipite kwa wina aliyense wa inu monga choncho. Ngati ine sindikwanitsa kuchita izi, M'bale Wagner, tsiku lina mbali inayo,

basi kumbali inayo, ine ndikufuna zaka chikwi, kumugawira, mmodzi aliyense wa inu. Chotero ife tidzakakhala ndi nthawi yopambana Kumeneko!

¹⁰ M'bale Toy, iye ndithudi, iye basi... Ine sindikumvetsa mmene iye amachitira zinthu zambiri mbiri pakamodzi, koma ndithudi iye amatha kuchita zochuluka kwambiri. Ine ndinamuwona iye tsiku lina ku kadzutsa wa Amuna Amalonda, mmene iye amatengera gawo la mlaliki, dikoni, wosamalira pamalo, ndi chirichonse chimene chimabwerapo, ndipo iye anali kuyesetsa kuti achite zonsezo. Iye amawakonda Ambuye. Ine ndinali ndi mwayi wokumana ndi mkazi wake, ndi kumuwona mwana wake wamkazi wokonedwa ndi mwamuna wake akuyimba. Izo ndithudi zinali zodzoza. Ine ndimanena posakhalitsapa ndi iye, mphindi pang'ono zapitazo, "Iwo sakuwona kuti azikhala pakhomo, kumagwira ntchito zawamba. Iwo akuyenera kuti azikakhala kunja uko ku munda wa uvangeri kwina kwake, ndi mphatso zapamwamba monga choncho."

¹¹ Mwaona, aliyense ali, ine ndikuyembekeza sindikumusiya aliyense. Dona amene amaimba limba, oyimba, makwaya, ndi onse amene akhala alipo, ine ndithudi ndikuyamikira izo ndi mtima wanga wonse.

¹² Ndi anyamata kuno, Gene ndi Leo, iwo akufuna kufotokoza kumverera kwawo kwa inu, nawonso, chifukwa chogula matepi ndi mabuku, ndi gawo limene iwo akuyenera kusamalira. Ine ndinakumana nawo iwo pa khomo, mphindi pang'ono zapitazo, ndipo ine ndinawauza iwo kuti ndidzafotokoza kumverera kwawo kwa inu anthu. Iwo ndithudi akuyamikira chirichonse chimene inu mwachita powathandiza iwo ndi kuyenda kwakukulu kwa Mulungu.

¹³ Ndipo tsopano ichi chikuchokera kwa inemwini, mwana wanga wamwamuna, mkazi wanga, ndi mpongozi wanga wamkazi, ndi onse. Ambiri, winawake wakhala akunena kuti, "Mlongo Branham ndi wuti?" Ameneyo ndi mtsikana wamanyazi kwambiri amene ine ndinayamba ndamuwonapo mmoyo wanga wonse. Oh, mai!

¹⁴ M'bale Art Wilson, ine ndikutsimikiza nonse a inu mukumudziwa iye. Ine ndikukhulupirira anali m'bale... Ayi, anali M'bale Jewel Rose, usiku wina, anati, "Ife tikufuna Mlongo Branham abwere pa nsanja," ndipo iye anangokhala ngati adwale mtima. Iye basi... Iye ndi wamanyazi kwenikweni.

¹⁵ Wokonedwa, ngati iwe sukomoka, iwe ungangomirira kwa miniti chabe, kuti winawake awone mtsikana wokoma amene ine ndinamukwatira. Chabwino. [Osonkhana akuomba mmanja—Mkonzi]. Mpongozi wanga wamkazi, mkazi wa Billy, Loyce, iwe ungaimirire, Mlongo, mphindi chabe. Ameneyo ndi mkazi wa Billy, [Osonkhana akuomba mmanja] ndi mpongozi wanga wamkazi.

¹⁶ Ambiri a inu mwamvapo za Joseph. Si choncho inu? Anthu aku Afrika posachedwapa anamutumizira iye chikhotho chaching'ono cha mangamanga. Ine ndinamuwona iye zaka sikisi iye asanabadwe, pamene adokotala anati ife sitidzakhala konse ndi mwana wina, ife timalephera kukhala naye. Ana athu amabadwa kudzera opareshoni. Amayi anga, abale a mkazi wanga amachita mwanjira imeneyo, iwo, ana awo onse amadzera opareshoni. Ndipo Ambuye anandiuza ine kuti ndikhala ndi mwana uyu, pamene adokotala anadzanena kuti izo sizingachitike, anati izo sizingachitike basi. Ine ndinati, "Izo zichitika, mulimonse." Ndipo ife tinadikirira zaka foro, masomphenyawo atabwera kale kuti ine ndikhala ndi mnyamata, ndipo ine "ndidzamatichule dzina lake 'Joseph.'"

¹⁷ Ndipo, zitachitika zimenezo, panali mtsikana wina amene anabadwa. Aliyense ankandiseka ine, ndipo ankati, "Iwe umatanthauza 'Josephine.'"

¹⁸ Ine ndinati, "Ayi. Ine ndimatanthauza 'Joseph,' ngati mnyamata." Iye mwinamwake adzatenga malo anga ine ndikadzapita, ngati Yesu achedwa. Ndipo zaka zina foro; ndiye adokotala anali wotsimikiza kuti sipakhalanso wina; zaka zina foro, Joseph anadzafika.

¹⁹ Ine ndikudabwa, amayi, ngati inu mungamunyalire iye mmwamba miniti chabe. Ine ndikufuna kuti iwo awone chimene... Mnyamata uyu ali kale ndi mzimu wa uneneri pa iye. Ndipo iye... Imirira pang'ono chabe, Joseph. Ndi ameneyo. Chabwino. [Osonkhana akuwomba mmanja—Mkonzi]. Iye ali ngati amayi ake, wamanyazi.

²⁰ Ine ndikuuzani inu chimene chinachitika. Ife tinali titachokapo... Iye ali usinkhu wa zaka foro tsopano. Koma pamene iye anali ndi zitatu, ife tinali titachokapo. Ndipo iye anati, "Adadi?"

Ndipo ine ndinati, "Inde, wokondedwa."

²¹ Iye anati, "David..." Ameneyo ndi mnyamata amene anali wolumala, ndipo anachiritsidwa, mwana wamwamuna wa Bambo Wood amene amakhala pafupi ndi ife. Anati, "Ine ndinali... ndinamuwona iye atachita ngozi pa njinga yamoto." Iye alibe ngakhale njinga ya motoyo. "Ndipo iyo inadzavulaza mwendo wake, iye anang'amba zovala zake ku mbali yakumanja."

Ine ndinati, "Zimenezo zinachitikira kuti, wokondedwa?"

²² Anati, "Kumusi kwa msewu kuchokera kumene ife timakhala." Ndipo masiku atatu kenako, mnyamata anadzabwera kuchokera ku Kentucky, atakwera njinga yamoto, ndipo David anapita kumusi kwa msewu ndipo anadzavulala mbali yake ya kumanja ndipo anadzang'amba zovala zake, basi monga Joseph anaziwonera izo.

²³ Pamene ine ndinkamupereka iye kwa Ambuye, mmawa, panali ana ambiri ataima, ndipo anali limodzi ndi amayi awo pa guwa. Pamene ine ndinadzamunyamula Joseph mmanja mwanga, ndisakuganizira chimene ine ndimanena, ine ndinati, “Joseph, mwana wanga, iwe ndi mneneri.” Limenero ndiro pemphero langa, mulimonse, ndipo ine ndikukhulupirira kuti izo zidzatero, kuti, Mulungu adzatenga chirichonse chimene Iye anandipatsa ine, ndipo adzachelukitsa izo pawiri, ndi kudzaziika izo pa mnyamata ameneyo, ndiye ine ndikadzachoka iye adzatenga malo anga.

²⁴ Billy wakhala ali mzanga. Ine ndamulera iye; amayi ake anamwalira pamene iye anali ndi miyezi eyitini yokha; ndipo ndakhala ndiri bambo ndi mayi, ziwiri zonse, kwa iye. Koma iye amawoneka kuti alibe mayitanidwe okhala mlaliki. Iye ndi wamanyazi, wofatsilira, ndi zina zotero, zambiri ngati amayi ake, wamanyazi. Koma iye wakhala thandizo lalikululu kwa ine mu msonkhano, chifukwa ine ndamudalira iye, ndimamutengera iye kunjira uko ndi kukamupatsa iye ntchito yoti achite. Mwaona, ntchito ya khadi la pemphero iyo ndi ntchito yoti uzidalirika. Winawake anaigwira iyo ndipo anati . . . Mwamuna nthawi ina anati, “Ine ndikupatsa iwe madola faifi handiredi ngati iwe ungakamuike mkazi wanga pa nsanja.” Nanga bwanji ngati zimenezo zitachitika? Ndiye Mzimu Woyera ungatani? Billy amadziwa bwino kwambiri kuti asayesere kuchita zimenezo. Iye amadziwa kuti ine ndikhoza kudziwa izo mwachangu iye akamafika pa nsanja, chotero, Ambuye akhoza kuulula izo. Ndi chifukwa chake iye—iye sangayerekeze kuchita zimenezo, chotero ndiye ndife tonse othokoza kwa iwe.

²⁵ Ndiyeno kwa woyang’anira pamalo ano, mwamuna amene amatithandizira ife pa chipata apo, ndipo ine ndikuganiza iye ali ngati woyang’anira pano, kapena chinachake, kapena mlonda pa chipata. Ndi anthu onse amene anatiloleza ife kukhala ndi malo olankhuliramo awa, ine sindinganene basi kuti “zikomo” mokwanira. Ine ndithudi ndikuyamikira zimenezo, ndipo onse amene ali muno mwanjira iliyonse, ndi chirichonse chimene chachitidwa.

²⁶ Tsopano iwo anandiuza ine, M’bale Borders, kamphindi kapitako, kuti iwo ananditengera ine chopereka chachikondi. Ine ndikuyamikira zimenezo, ndipo ndi mtima wanga wonse. Ine ndichigwiritsa ntchito icho, mwakupambana kwa kudziwa kwanga, kwa Ufumu wa Mulungu. Tsopano, si zimene timasunga kuno zimene zimawerengedwa, ndi zimene ife timatumiza kuti zizipita. Ndiye ndine wotsimikiza kuti Mulungu adzasungitsa izo mu akaunti yanu mu Ufumu umene uli nkudza.

²⁷ Tsopano, ine ndiribe purogramu ya walesi. Ine ndiribe chirichonse chogulitsa. Koma ngati inu mungafune umodzi wa mipango iyi kapena chinachake choti chipemphereredwe,

mundilembere ine ku Jeffersonville, Indiana, Post Office Box 325. Icho chikatunikiridwa, ndi ineyo, ndipo chidzatumizidwanso kwa inu. Ndipo ine ndimakhulupirira mu utumiki umenewo. Ndiyeno ngati inu mungafune kuti mundiimbire ine, BUtler 2-1519 ikandipeza ine ku Jeffersonville, Indiana. [Nambala ya telefoni inasinthidwa.—Mkonzi]. Chotero, kapena ngati inu simungaganize za izo, mudzangofunsa za ine ku Jeffersonville, iwo adzandiimbira. Tsopano, ine sindimachita izo kuti ndipeze adiresi yanu, chifukwa ine ndamavutika kuti ndimupeze winawake woti azindiyankhira makalata, ndi zina zotero. Ndipo tsopano ine sindiri mochuluka. . . Izo ziri bwino, ine ndimakhulupirira mu mapurogramu awa. Chirichonse chimene chiti chimuthandizire Mulungu, mudzichisiya icho chizikhala.

²⁸ Koma, inu mukudziwa, ine ndimamverera chonchi, kuti membala wa mpingo, ntchito yawo yoyamba ndi, ndi chakhumi chawo ndi zopereka, azithandizira tchalitchi chawo. Ngati inu muli mamembala a matchalitchi abwino awa amene aimiridwa pano, inu muzikathandizira tchalitchi chanucho. Ndiyo ntchito yanu yoyamba kwa Mulungu. “Kubweretsa chakhumi chanu ndi zopereka ku nyumba yosungira.” Ndipo nyumba yosungira, inu ndithudi mukuidziwa chimene iyo ili, ndi kumene inu mumakatengako chakudya chanu. Chotero, kumeneko ndi kumene inu mumakatengako chakudya chanu chauzimu, ndipo udindo wanu ndi wa kwa tchalitchi chanu ndipo osati kwa mvangeri ngati ine.

²⁹ Chimenecho chimatoleredwa kwinkwawake mmisonkhano pamene ife tikukhala ndi misonkhano yokopa anthu monga chonchi, pamene inu mumaika chochepa pambali kuti chikathandizire zimenezo, chimenecho chimandisamalira ine. Ndipo ine ndikukuthokozani inu kwambiri. Ndipo nthawi iliyonse, zovala zopemphereredwa kapena chirichonse monga choncho, mwamtheradi ndi zaulere. Simumakhala chirichonse mwa izo nkomwe, ife siti. . .

³⁰ Ndipo mabukhu athu, ndi zina zotero, ife tikamagulitsa izo, izo zimakhala. . . Ife timagula izo, forte peresenti motsika kuposa mmene ife timapezea izo, ndiyeno ife. . . ndizo, zikamadutsa kumeneko, kumakhala zambiri zowonongeka pa izo, ndipo pamakhalanso kulipira zotumizira pambali pa zimenezo, kenako inu mumayenera kuti muwabweretse iwo kuno ndipo kenako nkuwagulitsa iwo. Bwanji, inu simungakwanitse, inu simungakwanitse kupindula nkomwe ndi izo ngati inu mutafuna, mwaona. Koma ife timachita zimenezo basi chifukwa chakuti timafuna kufikitsa Uthenga kwa inu, kuyesetsa kuti inu muthandizidwe, inueni; ndiyeno kumuuzwa winawake, ndi kupereka izo kwa iwo. Icho ndi chifukwa chimene ife timakhalira ndi zinthu izi, sichoncho izo? Chikominsi chimapereka mabukhu awo ndi zowerenga

zawo, mwaulere, chifukwa iwo ndi ulamuliro wamphamvu. Ine ndangokhala munthu mmodzi. Ndikukhumba ndikanatha kutero, ndikanakhala ndi ndalama kuti ndizingoti “mabukhu onse ndi chirichonse, ndizauulele,” ine ndingachite zimenezo. Koma ine sindingachite zimenezo, ine ndimayenera kuti ndizikhala ndi chinachake choti ndizibwererakonso ndi kukadinda ena ochuluka, kapena—kapena kukagula ena ochuluka.

³¹ Ambuye akudalitseni inu. Ndipo inu muzindipempherera ine, sichoncho inu? Ndipo pamene ine ndiri kutsidya kwa nyanja, ndipo mmalo a mdima amenewo kumene asing’anga amaima ku dzanja lirilonse, kumakutsutsa iwe chirichonse chimene unganene, nthawi zikukhala zovuta, mphepo zotentha za chisautso zikuwomba, kodi ine ndikuikeni inu pa mndandanda, kapena inu mundiika ine pa mndandanda wanu, ndipo ine ndizikakumbukira pamene ine ndikukakumana ndi kutsutsa kuja kwa asing’anga ndi ziwanda, ndi zinthu kunja uko mmunda, ine ndikhoza kukati, “San Jose ikundipempherera ine”? Inu mutero, inu mukachita zimenezo? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati inu mungatero, munene, “Ine ndidzakhala ndikukupemphererani inu.” Zikomo inu. Zikomo inu, abale anga. Zikomo inu. Ine ndabwera pakati panu, kuti ndidzakhale m’bale wanu, ndi kubweretsa... kudzathandiza kubweretsa mtendere ndi Khristu, chirichonse chimene chiri chabwino kwa inu. Inu mundipempherere ine. Ngati ine ndamuiwala aliyense, mundikhululukire ine, ine sindikutanthauza kutero. Koma “zikomo” wamkulu wa pansu pa mtima, ndi madalitso a Mulungu kwa aliyense wa inu.

³² Ife tizinyamuka kupita kwathu tsopano, pompano. Ine ndikakhala ndi pafupifupi msonkhano wa masiku atatu kumeneko mu tchalitchi changa chaching’ono, kuwaphunzitsa iwo ubatizo wa Mzimu Woyera, kuyankhula mmalirime, zizindikiro ndi zodabwitsa zoti ziziwatsatira okhulupirira, ndi zina zotero; za anthu amene ali kozungulira, kumeneko.

³³ Ine ndimakhulupirira mu mphatso zonse zauzimu. Ine ndimakhulupirira mu Baibulo lonse. Ndine wa Pentekoste kuyambira pamwamba pa mutu wanga mpaka pansu pa mapazi anga, mkati, kunja, kuzungulira paliponse, kudutsa. Ndine wa Pentekoste! Inde, bwana! Iwo amati, “Ndinu wa ‘Baptisti,’ inu munatero.” Ndine wa Pentekoste Baptisti. Ndine wa Baptisti amene ali ndi Mdalitso wa Pentekoste. Chotero ndine... Ine ndimawakonda Ambuye Yesu.

³⁴ Ndipo ine ndinali kulalikira... Ndinakumana ndi azimzanga ena ochokera ku Arkansas, kunjako, ndipo ife tinali tikuyankhula za Arkansas. Ndipo ku Little Rock, usiku wina pamene... Uko kunali m’bale wachikulire wa Nazarene amayendera ndodo, ndipo iye ankagulitsa mapensulo pa msewu,

kwa zaka. Ndipo apa iye anali uko pa msewu, tsiku lotsatira, ndi ndodo zakale izi, akuyenda chokwera ndi chotsika pa msewu, basi akungolemekeza Mulungu. Usiku umenewo iye anali. . . Robinson Memorial Auditorium, anthu inu amene mukuchokera kozungulira Little Rock mukudziwa kumene iyo ili. Ndipo—ndipo iye anakweza mmwamba dzanja lake, ndipo anati, “Miniti chabe, M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake.”

Ine ndinati, “Inde, bwana, icho ndi chiyani?”

³⁵ Ndipo iye anati, “Inu mukudziwa, pamene ine ndinakumvani inu mukulalikira, ine ndinali wotsimikiza kuti inu ndi wa Nazarene.” Chifukwa, chimenecho ndi chimene iye anali. Iye anati, “Ine ndinali wotsimikiza kuti inu munali wa Nazarene, chifukwa inu mumalalikira chimodzimodzi ngati wa Nazarene.” Ndipo anati, “Kenako ine ndinakumvani inu mukuti inu munali membala, pa nthawi imeneyo, wa mpingo wa Baptisti.” Ndipo anati, “Osonkhana anu onse, pafupifupi, ndi a Pentekoste.” Anati, “Ine sindikumvetsa zimenezo.”

³⁶ Ine ndinati, “Chabwino, zimenezo ndi zophweka. Ndine wa Pentekoste Nazarene Baptisti.” Chotero ndicho chimene izo ziri. Chinthu chonsecho ndi ichi: ife ndi amodzi, mwa Khristu Yesu, omangidwa ndi msinga za chikondi Chake.

³⁷ Tiyeni tipemphere tsopano tisanatsegule Mawu, ife sitikufuna kuti tikusungeni inu motalika kwambiri tsopano kuwopera kuti muchedwa ku msonkhano wanu wa tchalitchi usikuuno. Koma tiyeni timufunse Mulungu tsopano kuti abwere ndi kudzatidalitsa ife, mopitirira, mochuluka. Ndi angati amene ali ndi chopempha tsopano, kwezani manja anu ndipo munene, “Ambuye Mulungu, Inu mungondikumbukira ine, ndine—ndine wosowa lero”? Mulungu akhale nanu.

³⁸ Atate akumwamba, pamene ife kamodzinso tikuyandikira Kukhalapo Kwanu Koyera, ife f- . . . ayi, ndipo, tikungomverera ngati tivule nsapato zathu, koma ife tikuvula mtima wathu ndipo tikungowuika iwo pamaso Panu, Atate. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha zonse zimene Inu mwachita mu msonkhano waukulu wokopa anthu uwu. Ife tikuzindikira, Ambuye, kuti ukulu sumatanthauza chiwerengero. Ukulu ndi Kukhalapo Kwanu. Pakuti, kunalembedwa zokhudza Mesiya wakudza, kuti “malo onse okwera adzatsitsidwa, ndipo malo otsika adzakwezedwa; masamba adzawomba mmanja mwawo, ndipo mapiri adzadumphira ngati ana ankhosa.” Ndipo munthu akhoza kulingalira mu kuganiza kwake kwaluntha, za nthawi yopambana imeneyo imene idzakhale, agaleta amoto amenewo adzabwera kuchokera Kumwamba, akumubweretsa Mesiya. Koma kodi izo zinachitika motani? Kwa mlaliki wokalamba wowoneka—mwamasanza, akubwera kuchokera ku chipululu cha Yudea, wosavala nkomwe ngati mtumiki; ali ndi chidutswa

cha chikopa atazikutira, ngati—nsalu; tsitsi liri paliponse pa iye, ndipo ndevu zake ziri pa nkhope yake; akulalikira, osati mu tchalitchi, koma pamagombe a Yordani, akufuula, “Lapani, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira!” Akuyenda chotsika mmagombe a matope, panabwera mphondero za Kalipentara waku Galileya, amene anadzayenda kukalowa mmadzi, ndipo Mulungu anazindikira izo ndipo anazilemekeza izo mpaka Iye anatsegula Miyamba ndipo iwo anawona Mzimu Woyera ukutsika ngati nkunda pa Iye. Izo zinali zopambana. Chimene munthu amachitcha “chachikulu,” nthawizina ndi chopusa pamaso Panu, Ambuye. Koma chimene munthu amachitcha “chopusa,” ndi chachikulu pamaso Panu.

³⁹ Tsopano ife tiri okondwa kwambiri kuti chinthu chachikulu chachitika mu San Jose. Apa pakhala atumiki amene akhala apa, ena a iwo ndi a Assemblies of God, ena a iwo ndi a Church of God, Independent, ndi United Pentecostal, ndi mitundu yonse yosiyanasiyana. Ndipo apa ine ndaima pakati pawo, osati kukhala wa lirilonse la bungwelo, koma ndikuyesetsa kuima pakati, kuyankhulira onse. Ndipo ife ndi amodzi, mwa Inu; mtima umodzi, chimvano chimodzi, malo amodzi. Ndi nthawi bwanji kuti Mzimu Woyera ukonzenso chinachake! Perekani izi, Ambuye. Inu mukhale ndi ife, Ambuye. Mudalitse chipembedzo chirichonse chimene chaimiriridwa pano. Perekani izi, Atate. Atumiki abwino onse awa, mulole mipingo yawo ikakule ndipo izikachita bwino, Ambuye. Mulole odwala achiritsidwe, akhungu akawone, osamva akamve, ochimwa apulumutsidwe ndipo adzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Mulole pakakhale kusefukira kwa chitsitsimutso kudutsa dziko lino pano, chimene chiti chidzagwedeze Gombe Lakumadzulo lonse. Perekani izi, Ambuye. Mulole pakhale changu chotere pakati pa abale anga, kuti iwo basi akalephere kupumulira; wina akamuyatsire winayo, ndipo mpingo uliwonse ukapite chitsogolo ngati gulu limodzi lalikulu, kukhala ndi chiyanjano wina ndi mzake, kunyema mkate nyumba ndi nyumba, ndi mtima umodzi. Perekani izi, Ambuye. Mutumize chitsitsimutso chimenecho chimene ife tikuchidikirira.

⁴⁰ Dalitsani osonkhanawa, pamene iwo akudikirira masana ano machiritso awo, ndi ambiri pa chipulumutso chawo. Ndipo ndithandizeni ine, O Mulungu, pamene ine ndikuwerenga kuchokera mu Mawu Anu opatulika. Mulole Mzimu Woyera utenge icho chimene chiri Chanu, Ambuye, ndipo muchibweretse icho ku mitima yathu. Ndipo kenako mundigwiritse ine ntchito, Ambuye, kuti ndipereke gawo lokhutitsa la Mawu Anu kwa mtima wa njala wina uliwonse. Ndimvereni ine, ine ndikupemphera, Atate, mu Dzina la Yesu ndikupempha izi. Amenii.

⁴¹ Winawake wangondipatsa kumene ine kacholembedwa kakang’ono, ndipo akuti, “M’bale Baxter, wochokera ku

Canada, akutumiza chikondi chake ndi moni kwa inu, ndipo iye ali kuno mu California tsopano, akuchititsa msonkhano ku Concord.” Mulungu amudalitse M’bale wathu Baxter. George Patterson, kodi muli pano? George Patterson, kodi muli mu msonkhano? Ngati inu muli, mutenge chikondi changa... Mulungu akudalitseni inu, M’bale Patterson; mutengere chikondi changa kwa M’bale Baxter, mwamuna wabwino. Ndipo ngati aliyense wa inu mukakhale pafupi ndi kumeneko, ngati inu mukufuna kuti mukamve ulaliki wolalikidwa ndi mwamuna amene amadziwa kuchita izo, mupite mukamumvere iye, ngati mukakhale pafupi ndi kumeneko; ndithudi ndi mlaliki wodabwitsa. Ife tinakhala limodzi kwa zambiri, zaka zambiri. Chikondi changa sichinayambe chafapo pa M’bale Baxter; icho sichidzatero konse. Iye ali ndi tchalitchi chachikulu mu Canada. Iye sakanakwanitsa kuti azikhala ndi ine kenanso, chifukwa chalitichi chake chimamufuna.

⁴² Ine ndikudziwa chimene izo ziri. Ngakhale Kachisi wanga lero, kumene kuli maziko anga... Tsopano, anthu amene amatumiza zithandizo kwa utumiki uwu, ali ndi nambala ya boma imene imabwerera kwa inu, kuti asamakuduleni msonkho pa chirichonse chimene mumatumiza kwa utumiki uwu. Iwo ndi u—utumiki wosapanga phindu, wotchedwa Branham Tabernacle. Ndipo ine ndikudziwa, kumeneko, ma trastii awo amandipanikiza ine, “Tiyeni timange kachisi wamkulu, inu muzikhala pano ndipo anthu azibwera kwa inu.” Zimenezo zimamveka zabwino, koma zimenezo si chifuniro cha Mulungu kwa ine. Pali anthu ena amene alibe ndalama zokwanira kuti azibwera kwa ine, ine ndimayenera kuti ndizipita kwa iwowo. Mukuona? Chotero ine—ine ndikudziwa chimene chimakhala iwe ukamapanikizidwa.

⁴³ Ndipo M’bale Baxter anaikidwa zimenezo pa iye, chotero iye anasiya ntchito ya misonkhano ndipo anapita ku tchalitchi chake. Ambuye amudalitse M’bale wathu Baxter. Mumutengere iye chikondi changa ndi moni, kwa iyeyo, wa ine, ngati inu mungatero, m’bale.

⁴⁴ Tsopano tiyeni titsegule Lemba, kwa pafupifupi maminiti twente otsatira, kwa ena a Mawu, amene, Iwo sadzalephera konse. Ndipo anthu onse amene muli pano, odwala, osowa chirichonse, mungozilola nokha mulowe mu Mawu molunjika. Ine ndinali woti ndilalikira masana ano pa *Momwe Mphungu Ikasulira Chisa Chake*, koma, ine ndinadzapeza kuti, anyamatawo anali nawo iwo kuno ndipo agulitsa iwo pakati pa anthu, mmaonekedwe a bukhu. Ndiyeno, pokhala wosasa mawu pang’ono pa mmero panga, ine ndinatenga phunziro lina. Ndipo ine ndikuganiza tsopano ine ndayankhula chirichonse chimene ine ndimayenera kuti ndiyankhule. Chabwino. Tiyeni titsegule ku Yohane, Yohane Woyera, mutu wa 14, pa kuwerenga

kwathu kwa Lemba. Ndipo mvetserani mwatcheru pamene ife tikuwerenga ndime eyiti zoyambirira za Yohane 14.

Mitima yanu isavutike: inu mukukhulupirira Mulungu, mukhulupirirensa mwa ine.

Mu nyumba ya Atate anga muli nyumba zambiri: ngati sizikanakhala chomwecho, ine ndikanakuuzani inu. Ine ndikupita ndipo ndikukakukonzerani inu malo.

Ndipo ngati ine ndikupita kukakukonzerani inu malo, ine ndidzabweranso, ndipo ndidzakulandirani inu kwa inemwini; kuti kumene ine ndiri, inunso mukakhale.

...kumene ine ndikupita inu mukudziwako, ndipo njirayo inu mukuidziwa.

Tomasi anati kwa iye, Ambuye, ife sitikudziwa kumene inu mukupita; ndipo ife tingaidziwe bwanji njirayo?

Yesu anati kwa iye, ine ndine njira, choonadi, ndi moyo: palibe munthu angadze kwa Atate, koma podzera mwa ine.

Ngati inu mukanandidziwa ine, inu mukanawadziwanso Atate anga: ndipo kuyambira pano inu mukundidziwa ine, ndipo mwandiwona ine.

Filipo anati kwa iye, Ambuye, tiwonetsereni ife Atate, ndipo icho chitikwanira ife; mwakuyankhula kwina, tikhutsidwa.

⁴⁵ Tsopano ndicho chimene ine ndikufuna kuti ndiyankhulepo, masana ano. Kwakhala kuli kulira kwa mtima wa munthu, kwa a... chiyambireni pamene ife tinakhala anthu, ife timafuna kumuwona Mulungu. Ndipo ine ndikufuna kuti nditenge pafupifupi njira zinayi, masana uno, kuti ndikuwonetseni inu Mulungu. Choyamba ine ndikufuna kumutenga Mulungu mu chirengedwe Chake, Mulungu mu Mawu Ake, Mulungu mwa Mwana Wake, Mulungu mwa anthu Ake. Ndipo ife tikhoza kuzitenga izo njira zina zambiri. Koma ine ndikufuna kuti ndiyankhule kuchokera pa maphunziro foro amenewo, njira foro zosiyanasiyana zimene ife titi tiyang'anepo, kuti tiwone ngati tingathe kumuwona Mulungu. Tsopano, palibepo munthu pano koma amene angafune atamuwona Iye. Kodi inu simungafune mutamuwona Mulungu? Ine ndimafuna nditamuwona Iye. Chotero ngati Iye ali Mulungu, chimene ife tikudziwa kuti Iye ali, ndiye nchifukwa chiyani tikulephera kumuwona Iye?

⁴⁶ Yobu nthawi ina ananena kuti, Bukhu lakale kwambiri mu Baibulo, ananena chinachake chonga ichi, "Ngati ine ndikanangodziwa kumene Iye amakhala, ine ndikanapita ndi kukagogoda pa khomo Lake. Ndipo ine ndikufuna kuti ndikayankhule naye Iye." Ndipo iye anayamba kuyankhulana ndi Mulungu. Mulungu anamuza iye kuti adzimangire yekha

ngati mwamuna, pakuti Iye anali woti ayankhulana naye iye. Ndipo Iye anatsika pansu mu kamvulumvulu, ndipo anayankhula ndi Yobu.

⁴⁷ Zikundikumbutsa ine za... uko pafupi ndi malo athu. Iye timakhala ku Mtsinje wa Ohio. Ndipo uko kunali mnyamata wamng'ono amene anapita ku Sande Sukulu inayake, Sande Sukulu ya Baptisti, mdziko lathu, ndipo iye anatengeka kwambiri. Tsiku lina pamene anawafunsa amayi ake, “Ngati Munthu wamkulu uyu amene amatchedwa Mulungu, amene ife timapita ku tchalitchi kukamupembedza, ngati Iye ali ngati Munthu wopambana chomwecho, ndikudabwa ngati inu mungandilole ine ndimuwone Iye? Ine ndikufuna nditamuwona Iye.”

⁴⁸ “Oh,” amayiwo anati kwa mwana wawo wamng'ono, iwo anati, “chabwino, mwana, iwe uyenera kuwafunsa aphunzitsi ako a Sande Sukulu, amayi sangakwanitse kukupatsa yankho limenelo.”

⁴⁹ Chotero ku Sande Sukulu iye anayankhula ndi aphunzitsi ake, ndipo iye anati, “Ine sindingathe kukupatsa chimenecho, nanenso, chotero bola iwe ukawafunse abusa.”

⁵⁰ Ndipo utatha ulaliki, iwo anawafunsa abusa. Ndipo abusa anati, “Ayi, mwana.” Anati, “Palibe munthu amene angamuwone Mulungu.” Anati, “Mulungu ali ngati mpweya, ndipo iwe sungathe kumuwona Iye.” Ndipo, ndithudi, izo sizinamukhutitse mwanayo.

⁵¹ Ndipo iye anakakonda kucheza ndi bambo wokalamba kumusi kwa Mtsinje wa Ohio. Ndipo iye anali nsodzi weniweni wokalamba, imvi mu ndevu zake, ndipo usinkhu wa zaka zina sikisite-faifi, sevente zakubadwa, akulongedza, amakhala mu ngalawa yaing'ono yachikale. Ndipo ine ndinawedzapo ndi iye, inemwini, ndipo ife tinkakonda kupita kumtunda uko kuzungulira zisumbu ndi kukawedza, tinkatchera zingwe. Chotero mwana uyu anali ndi iye tsiku lina, kumtunda kwa mtsinje. Ndipo ali panjira akubwerera, panadzabwera nkuntho ndipo iwo amayenera kuti athamangire msanga ku gombe, kuti akakocheze ngalawa yaing'onoyo, chifukwa mafunde anali atakula kwambiri akuwopsya ndipo athovu pamwamba, kufikirira kuti iwo akanakhoza kugudubuza bwatolo. Chotero nkuntho utatha, ndipo iwo anadzabwera kuseri kwa mitengo, anakankhira ngalawa yaing'oyo kuchoka pa gombe, ndipo inakalowa mmathithi a mtsinje, umene unali pafupifupi mailosi imodzi kupingisa Mtsinje wa Ohio kumeneko. Anayamba kumatsika ndi mtsinjewo, kumatsetserekerera limodzi, pamene nsodzi wachikulireyo anali kukoka nkhaifi.

⁵² Ndipo pamene iwo anali kuseri kwa mtengowo, nsodzi wakaleyo anali atamuza mnyamata wamng'onoyo nkhani (monga iye anamufunsira iye) chifukwa chimene iye anali wosakwatira, ndipo analibe aliyense woti azimusamalira

ieye. Ndipo iye anati, “Oh, mwana, pali Winawake amene amandisamalira ine. Ndipo chifukwa chimene ine ndiri wosakwatira, mkazi wanga ali Kumwamba, akundidikirira ine.” Ndipo iye anapitirira nayo nkhaniyo.

⁵³ Ndipo pamene iye anakalowa mmathithi, iwo anali akupita kummawa ndi ngalawa yaing’onooyo. . . kapena amapita kumadzulo, kani, ndi ngalawa yaing’onooyo, ndipo nsodzi wokalambayo akuyang’ana. . . akubwerera mmbuyo kuloza kumadzulo, zinali chakumadzulo, ndipo—ndipo dzuwa linali likukalowa. Ndipo, mvula ikatha, pamabwera utawaleza.

⁵⁴ Ndipo, oh, ine ndikuganiza imeneyo imakhala nthawi yokongola kwambiri! Pamene mvula yatsuka fumbi lonse kuchokera mmitengo, ndipo—ndipo iyo imawoneka yokongola kwambiri, ya girini, imakhala mmitundu yake ya pachiyambi. Ndipo maluwa onse amakhala okongola ndipo mlengalenga mumatsika, ndipo mumabweretsa kununkhira kwa maluwa. Iyo imangokhala nthawi yokongola basi, mvula ikakata.

⁵⁵ Ine ndikuganiza kuti izo mwanjiraina zikundikumbutsa ine, chitatha chitsitsimutso, pamene Mzimu Woyera unabwera ndi kudzatsuka fumbi lonse, ndi—ndi kudzaticometsanso ife pamaso pa Ambuye. Basi kungoima mu Kukhalapo kwa. . . monga mmene ine ndiriri masana ano, ndikungosamba pano mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu. Mzimu Woyera ukutichotsera ife kukaikira konse ndi mantha ndi zinthu, ndipo ife nkuima pamodzi, pambuyo pa—mivumbi yochokera Kumwamba itadzazitsa miyoyo yathu.

⁵⁶ Pamene nsodzi wokalambayo anayamba kukoka ngalawa yake, mnyamata wamng’onooyo anazindikira kuti misonzi inayamba kutsikira pansu pa nkhope ya nsodziyo. Ndipo mwanayo anapotoloka kuti awone chimene iye anali kuyang’ana, ndipo pamenepo panali utawaleza utapingasa mmwamba. Chotero mnyamatayo atakhala kumbuyo kwa ngalawa, anatengeka. Chotero iye anali atagwira mmbali mwa chingwe, ndipo iye anadzuka, ndipo anathamangira kumbuyo kwa ngalawayo ndipo anadzagwera pansu pa miyendo ya nsodzi wokalambayo. Ndipo iye anati, “ine ndikufuna ndikufunensi inu chinachake chimene amayi anga ngakhale mphunzitsi wanga wa Sande Sukulu, kapena abusa, sanandiyankhe ine.”

⁵⁷ Ndipo nsodzi wokalambayo anasiya nkhope yake, ndipo anati, “Icho ndi chiyani, mwana?”

⁵⁸ Iye anati, “Ine ndakuwonani inu mumayang’ana pa utawaleza uwo.” Anati, “Iwo amandiuza ine kuti Mulungu anawuika iwo pamenepo.”

Iye anati, “Izo nzoona, mwana wanga.”

Iye anati, “Ngati Mulungu ali wamkulu kwambiri, kodi aliyense angathe kumuwona Iye?”

59 Ndipo nsodzi wokalambayo anadzamukumbatira mnyamata wamng'ono pachifuwa chake, ndipo iye anati, “Madalitso pa iwe, mwana wanga wamng'ono! Ndilole ine ndikuuze iwe chinachake. Zonse zimene ine ndakhala ndikuziwona zaka fifite zapitazi zakhala ali Mulungu.”

60 Munali Mulungu wochuluka kwambiri mkatimo, mpaka kuti iye amatha kumuwona Iye kunjaku. Tsopano, imeneyo ndi njira yokhayo imene inu mungathere kumuwona Mulungu, ndikumutengera Iye mkati mwanu, kumulola Iye kuti aziyang'ana kupyolera mmaso anu, ndipo Iye adzadziwonetsera Yekha.

61 Ndithudi, Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake. Palibe amene amaganiza bwino amene angaganize za... Mukapita kuno ku Los Angeles, Mount Palomar, kwinkakwake, ndi kukayang'ana pa izo, zithunzi zija zimene iwo anajambula. Ndi malo aakulu oyang'anira zammwamba aja, kumene zaka handiredi ndi twente milioni za danga la kuwala zija, inu mukhoza kuziwona. Nkuziswa izo mmamailosi, ndi kuwona kumene inu mudzapite. Bwanji, inu mukhoza kuyendetsa mzere wa ma naini kuzungulira mzinda uwu, komabe osakwanitsa kuziswa izo mmamailosi. Koma kuseri kwa zimenezo kukadali kuwala kwa zammwamba, kumangopitirira! Ndipo pamene munthu ayang'ana pa zimenezo, pamakhala chinthu chimodzi chokha chimene iwe ungachite, ndicho kukwezera mmwamba manja ako ndikuti, “Bwanji,” kuyimba, “Ndinu wamkulu bwanji! Ndinu wamkulu bwanji!” Chirichonse chimazungulira mwangwiwo, mpaka kukhoza kukuuzani inu kadansana wa dzuwa ndi mwezi, zaka twente izo zisanachitike, mpaka ku miniti. Zoikidwa mu nthawi yake mwangwiwo ndi Mulungu!

62 Ndiyeno ngati inu mungazindikire mu chirengedwe, mmene Mulungu amasunthira pakati pa chirengedwe Chake. Mmene dziko linapendekekeranga pang'ono, kuti lizibweretsa mpweya wotentha ndi wozizira pamodzi, kuti lizipanga mvula imene imathirira mbewu zanu. Mmene Mulungu amakhalira mu chirengedwe Chake! Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndithudi, Iye amatero.

63 Ndipo nthawi ina yapitayo ine ndinali kuyankhula ndi munthu, pa phunziro la Mulungu. Ndipo kunali uko, mu Kentucky. Ndipo iye anati kwa ine... Iye anali wachikunja. Bambo Wood ndi ine tinali tikusaka agologolo, ndipo ife tinapita kuti tikamufunse ngati ife tingasake ku malo ake. Ndipo iye anati, “Oh, pitani,” iye anatero.

64 M'bale Wood anati, “Uyu ndi ine ndi anga—abusa anga, tikufuna tisake.”

65 Iye anati, “Wood, iwe sukutanthauza kuti iwe wapepera chomwecho mpaka iwe ukumachita kuyenda ndi mlaliki nthawi zonse?”

66 Ndipo iye anati, “Ayi, awa ndi abusa anga chabe.” Anati, “Iwo amakonda kusaka.” Ndipo anati ine. . .

67 Ndipo ine ndinakhala ndiri kunja kwa pafupifupi masabata awiri, ndevu zitalatika pafupifupi theka la inchesi; ndi—ndipo nditatuwa mmene ndikanathera, chifukwa chogona pansu, mmene ife timachitira msasa. Ine ndinali uko, ndikupumula. Ndipo umo ndi mmene ndimapumulira, chifukwa ine ndimamupeza Mulungu mu chirengedwe. Limenelo linali Baibulo langa loyamba, anali Mulungu mu chirengedwe Chake, mu zammwamba Zake.

68 Ndipo iye anati, “Chabwino,” iye anati “ziri bwino ndikuganiza, kuyanjana ndi alaliki.” Iye anati, “Koma, iwe ukudziwa, ine ndiri ndi lingaliro langa la zinthu zimenezo.” Iye anati, “Ine sindikhulupirira mu chipembedzo cha mtundu uliwonse.” Ndipo panali bambo wina atakhala ndi iye. Ndipo—ndipo ife tinapitirira, tikuyankhula za chipembedzo (iwo anatero) kwa kanthawi. Ndipo ine ndinangoima pamenepo, ndikudya apulo amene ine ndinamutola pansu.

69 Ndipo iye, bambo wokalamba uyu amene amayenera kukhala wachikunja, iye anati, “Ine kambiri ndakhala ndikudabwa. Ine ndikufuna ndidzakumane naye mlaliki wina.” Ndipo anati, “Ameneyo ndi amene anali kuno ku Acton, nthawi imeneyo.” Iye anati, “Inu mukudziwa, mlongo wokalamba kuno pa phiri; ine sindingathe kutchula dzina lake pakali pano.” Anati, “Mwamuna ameneyo anali ataima pamenepo pa Methodist Campgrounds,” mothandizidwa ndi mpingo wa Methodist. Zimenezo zinali zachirendo, koma izo zinachitika. Ndipo ife tinali ndi msonkhano wa machiritso.

70 Tsopano, inu a Methodist mukuyenera kukhulupirira zimenezo. John Wesley ankakhulupirira izo. Ndithudi, iye ankatero. Okonzanso onse oyambirira ankakhulupirira mu machiritso Auzimu.

71 “Ndipo,” iye anati, “ataima mu msonkhano usiku umenewo, iye anayankhula kwa mchemwali wake wa mkazi wokalamba uyu apa. Kuti mkazi wanga ndi ine ndi mwamuna wake, zonse zimene ife tikanachita (iye anali atatheratu ndi khansa, madokotala anali atamulephera iye, masabata ammbuyo), ndi kumuika iye pa machira mmawa umenewo.” Anati, “Iye anali mu chikhaliidwe chimenecho!” Ndipo anati, “Mchemwali wake anali pa msonkhano umenewo. Ndipo mlaliki uyu anatchula dzina la mkazi uyu, ndipo anamuza iye kuti abwere, ‘akaike mpango pa mkazi uyu amene anali ndi khansa,’ mchemwali wake. Ndipo iye anakatero, usiku umenewo. Ndipo mmawa wotsatira, iye anadya nyama ndi mazira, ndipo anaphika zitumbuwa zokazinga za apulo kukhala kadzutsa wake, ndipo anadya izo.” Iye anati, “Ine ndikufuna ndidzakumane naye mlaliki ameneyo tsiku lina.” Ine ndinangoima pamenepo.

Ndipo ine ndinati, “Kodi inu mungamudziwe mlaliki ameneyo?”

⁷² Iye anati, “Ayi, ine sindikumudziwa iye.” Ndipo M’bale Wood anandiyang’ana ine, ndipo anaphethira.

⁷³ Ndipo ine ndinati, “Kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti inu simumakhulupirira kuti kuli Mulungu?”

Iye anati, “Ine sindingakhulupirire izo pokhapokha nditaziwona izo.”

Ine ndinati, “Kodi mtengo wa apulo uwo uli ndi zaka zingati?”

“Oh,” iye anati, “Ine ndinaudzala iwo pamenepo pafupifupi zaka forte zapitazo.”

⁷⁴ Ine ndinati, “Pano ndi Seputembara koyambirira chabe, ife sitinakhale ndi nyengo yozizira kapena chirichonse. Ndiuzeni ine, bwana, ndi chiyani chimene chimayankhula, ndi Luntha lanji limene limayankhula ndi mtengo umenewo ndi kupangitsa utomoni umenewo kupita pansu ku mizu ndi kukadzibisa wokha ku chisanu? Muthire madzi pa chitsapo ndipo muwone ngati iwo angapange zimenezo, kapena muike odzadza mbale pa iwo, ndipo muwone ngati iwo angapite pansu ndi kukadzibisa okha mu nthaka, kuthawa nyengo yozizira. Ngati iwo sungachite zimenezo, nyengo yozizira ingaphe mtengowo nthawi yomweyo. Koma Luntha lina limapititsa utomoniwo pansu mu nthaka, kuchokera mu mtengo umenewo, ndipo umapangitsa iwo kukhala wofunda; kuchokera ku masamba, amene anagwera pansu, kuchokera mu mtengo. Ndipo dzinja lotsatira, nyengo isanayambe nkomwe kukhazikika, apa utomoni umabwereranso mmwamba, umabwera limodzi nawo moyo watsopano. Tafotokozani zimenezo kwa ine. Mundiuze ine chimene chimachita zimenezo.”

Iye anati, “Ine sindinayambe ndaganizirapo zimenezo nkale lomwe.”

⁷⁵ Ine ndinati, “Ndi Mulungu akukhala mu chirengedwe Chake. Mulungu amaika chirichonse molondola basi.”

Iye anati, “Dzina lanu ndi ndani?”

Ine ndinati, “Ndine M’bale Branham.”

⁷⁶ Iye anati, “Munthu wake ndi ameneyo, dzina—dzina la munthu amene anali kumeneko.”

Ine ndinati, “Izo nzoona.”

⁷⁷ Iye anati, “Ndi manyenje onsewo, ndipo utadzola magari a gologolo, ndi iweyo?”

Ine ndinati, “Izo ndi chimodzimodzi basi, ine, munthu wake ndi ineyo.”

Iye anati, “Iwe unamudziwa bwanji mkazi ameneyo?”

Ine ndinati, “Ine sindinatero.”

⁷⁸ “Iwe unadziwa bwanji kuti iye akhala bwino?” Anati, “Iye wangodutsa kumene kumusi kwa msewuku kuno, iye ndi mwamuna wake, kamphindi kapitako, akuyenda.”

Ine ndinati, “Ine sindimadziwa zimenezo.”

Anati, “Kodi iwe unamuchiza iye?”

⁷⁹ Ine ndinati, “Ayi, bwana. Mulungu anandiwonetsa izo, Mulungu anamuchiza iye, icho ndi chisomo Chake chodabwitsa!”

⁸⁰ Iye anali akudya apulo, ndipo iye anadzaluma. Ndipo iye anatembenuza mutu wake, anati, “Inu mukhoza kupita ndi kukasaka agologolo.”

⁸¹ Ine ndinayang’ana pozungulira, ndipo misonzi inali ikutsikira pansi mmasaya ake. Ine ndinadzaika nkono wanga pa iye, ine ndinati, “M’bale, inu mukumukhulupirira Iye, sichoncho inu?” Iye anagwedeza mutu wake monga *choncho*, ndipo anapotoloka ndi kumapita kubwalo la ku khola. Oh, Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake!

⁸² Nthawi ina yapitayo, wosakhulupirira anadutsa mu fukoli, zaka zapitazo, forte, fifite, zaka sikisite zapitazo, akutembenuza anthu. Oh, iye anali wanzeru kwambiri ndi luntha lake mpaka alaliki amakono, oyankhula mwaluntha, samatha kugwira chirichonse pa iye. Ndipo iye anawatembenezira anthu kukhala achikunja. Ndipo nthawi ina thanzi lake linafooka; iye anapita kumtunda ku Colorado, pafupi ndi kodyetsera ziweto kumene ine ndinkakonda kukadyetserako ziweto ndi kukagwira ntchito. Ndipo iye anali ali pa tchuthi chake kumeneko. Mwamuna yemwe ine ndimamudziwa, ndi bambo ake, anali atadulira a—njira zachidule, kuti akayike msasa wake. Ndipo tsiku lina iye anali akuyenda akutuluka, ndipo iye anadzaima. Ndipo anayang’ana pa miyalayo, ndipo iye anati, “Basi kodi inu munachokera kuti? Inu munafika bwanji pamenepo?” Ndipo mphepo zinayamba kuwomba. Iye anati, “Kodi ine ndakhala ndikulakwitsa nthawi yonseyi? Ngati Mulungu alipo, msiyeni Iye andiyankhule ine!”

⁸³ Pamenepo, wachikunja uja amene alaliki kapena aliyense panalibe—amatha kumuimitsa iye kapena kumugonjetsa iye, kani, mmawu a chidziwitso chake, koma iwo ankamuwopa iye. Koma Baibulo linati, “Ngati iwo angokhala chete, miyala mwamsanga idzafuula mokweza.” Mulungu ali nayo njira yochitira zinthu. Miyala inafuula mokweza! Pamenepo anagwada pansu, ndipo analozetsa nkhope yake ku nthaka, iye anagonjera mzimu wake wosakhulupirirawo kwa Mulungu, ndipo anadzakhala m’Khristu wokoma, wodzichepetsa. “Iwo akakhala chete, chirengedwe chidzafuula mokweza.”

⁸⁴ Ine, ndine msaki. Ine—ine ndimakonda kusaka, chifukwa kumeneko ndi kumene ine ndinamupezako Mulungu, koyamba, munali mu nkhalango. Pamene ine ndinkafunidwa kuti ndikamutumikire Iye koyamba, ine sindinkadziwa mmene ndingapempherere. Ndipo ife sitinkapita ku tchalitchi nkomwe; anthu athu, mmbuyo, anali...ine, ndinali wa Katolika. Iwo sanali...Wachi Irish, mwa chibadwa, amayi ndi abambo, awiri onse; kupatula, agogo anga aamuna anali Achimwenye. Ndiyeno iwo...Ine sindinkadziwa kupemphera. Ndipo ine ndinkafuna kuti ndipulumutsidwe, ndipo, inu mukudziwa chimene ine ndinachita koyambirira? Ine ndinakhala pansi ndipo ndinamulemba Mulungu kalata, ndipo ndinamuuza Iye kuti ndinali ndikupepesa chifukwa cha zimene ine ndinachita. Ndipo ine ndinali woti ndipita ku nkhalango, mu kanjira kamene ine ndinkakonda kukhala ndi kumverera kwachirendo kwenikweni ndikapita ku malo amenewa, ndipo ine ndinali woti ndikaikhomera iyo pa mtengo kuti Iye adzathe kuiwerenga iyo Iye akamadutsa. Chifukwa, ine ndinkadziwa kuti Iye amakhala kumeneko mu nkhalango penapake. Ine ndinali nditawona zinthu zambiri zikuchitika; ine ndinkadziwa kuti Iye amakhala penapake. Ndipo ine ndinaganiza, “Iye, pokhala wopanda tchimo, Iye akhoza kukhala uko kumalo amene anali oyera, ndi kumene kunalibeko anthu.” Iye akhoza...Ine ndikhoza kukamupeza Iye kumeneko mwabwinoko kuposa mmene ine ndikanachitira mmalo amene anthu anali atawawononga. Ine ndinaphunzira, Baibulo langa loyambirira linali kuchokera ku chirengedwe.

⁸⁵ Kapena, inu—inu mutenge abakha aang’ono awa. Iwo amachokera Kummwera kuno, ndipo amapita uko, amapita mpaka mu Canada, ndipo iwo amakapanga chisa chawo uko mmatope. Ndipo iwo amakaikira mazira awo, ndipo abakha aang’onowo amabadwa. Ndipo, kenako, mmenemo mumakhala mu dzinja. Chaka chimenecho, iwo amakhala akuleredwa, chirimwe chonse iwo amakhala akudyetsedwa. Ndipo pamene nthawi ya chisanu ifika, nthawi yoyamba pamenepo pamabwera mphepo yozizira imadzawomba mmapiri, kumene kumakhala chisanu, imadzasesa kutsika kudutsa dzikolo ku nyanja, kapena mapiri ammusi, ndipo kamphepo koyambirira kozizira ako kamene kamawomba kudutsa kumeneko, kokhala ndi chisanu mmenemo; penapake mu gulu lalikulu ilo la abakha mdziwe ili, pamakhala mtsogoleri wamng’ono, bakha wamwamuna wamng’ono. Iye amathamangira kunja uko pakati pa dziwe limenelo, nkudzadzutsa mlomo waung’ono uwo mmalere, ndipo amadzalira ka foro kapena ka faivi, bakha aliyense pa dziwelo amabwera kwa iye. Iye amadzuka kuchokera pamenepo. Iye sanayambe wachokapo pa dziwe limenelo; iye anabadwira mmenemo dzinja limenelo. Iye amadzuka kuchokera mu dziwe limenelo ndi kumangopita molunjika waku Louisiana mmene

iyе angapitire, ku minda ya mpunga iyo; wopanda namulondola nkomwe. Iwo amadzitcha izo “kununkhiza.”

⁸⁶ Ine kawirikawiri ndakhala ndikuganiza, ngati Mulungu angapereke luntha lokwanira kwa bakha, lotchedwa “kununkhiza,” kuti lizimutsogolera iye kuchoka ku mavuto, kodi Iye akuyenera kuchita chiyani kwa mpingo umene wabadwa mwatsopano, wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera? Kodi Iye akuyenera kuchita chiyani? Iye alibe namulondola, koma iye anabadwa ali mtsogoleri! Abakha amamudziwa mtsogoleri wawo, koma mpingo sumamudziwa. Mzimu Woyera ndiye Mtsogoleri wathu, Iye ndi Mphunzitsi wathu, Iye adzatitsogolera ife mu Choonadi, kikalowa Mmoyo. Abakha amamudziwa wawo, koma izo zimawoneka ngati nthawizina ife sitimakhala ndi luntha lokwanira ngati bakha. Chifukwa, iye amakonda kusunga chimene chaperekedwa kwa iye, koma ife timayesetsa kuganizira chinachake chosiyana. Zimenezo ndi luntha, inu mumachoka mu chirengedwe chachikulu cha Mulungu.

⁸⁷ Ine ndikuuzani inu chimene inu mungachite, ena a anthu inu ochokera ku maiko ozizira. Inu mukaiwona nkumba yayikazi yokalamba iyo ikupita kuchokera kumbali ya kumpoto kwa phiri, ndi kumatutira mankhosho onse awo ndi zitsononkho kumbali ya kummwera kwa phiri, ndi kukadzipangira bedi yake. Ndipo usiku umenewo inu mukamvetsera nkhani, ndipo nkhani nkuti, “Mawa, kukhala nyengo yabwino,” inu musalabadire nkomwe zimene iye akunena. Nkumba yayikazi yokalamba iyo imadziwa zochuluka za nyengo kuposa mmene iye angadziwire. Ndizo ndendende kulondola. Iyo yapita ku dera la kummwera kumene kudzakhale kofundirako.

⁸⁸ Inu mupite kokasaka akalulu ndipo mukawone akalulu amenewo atakhala uko pansu pa tchire, monga *chonchi*, akuyembekezera nyengo yozizira! Ndipo ngati inu muwawona iwo akukalowa mmunda wa chimanga, ikukonzekera kuti ivumbe.

⁸⁹ Mungomuwona Mulungu, Iye amayenda, oh, mmene Iye aliri wodabwitsa! Ngati inu mutangotsegula maso anu, inu mukhoza kumuwona Iye paliponse pokuzungulirani. Iye amakhala mu chirengedwe Chake, paliponsepo, amayenda. Muwoneni iye mu kulowa kwa dzuwa. Muwoneni Iye mu kutuluka kwa dzuwa. Muwoneni Iye mu utawaleza. Muwoneni Iye paliponse. Inu mukhoza kumuwona Iye, Iye sali kutali ndi inu kuposa mmene dzanja lanu lamanja liriri. Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake.

⁹⁰ Zaka zingapo zapitazo, ine ndinkasaka mphalapala, kumtunda mu Colorado kumene ine kawirikawiri ndimakasaka. Ndipo kumtunda mmapiri uko, zinali koyambirira kwa kugwa kwa masamba, ndipo chisanu chinali chisanabwere mwakuya kokwanira kuti chithamangitse mphalapala kuchoka

ku mitengo yaitali, kupita ku chigwa. Chotero Jeff ndi ine, wolondolera ziweto, ife tinali. . . Ine ndamuthandizapo iye kulondolera ziweto kwa zaka, ndipo ndimawathandizabe iwo panthawi yodyetsa. Ndipo ife tinali titakwera, kuti tizipita kokasaka, ndipo amatha kundichokera ine kwa masiku atatu kapena anayi. Iye anabwerera kumtunda ku mphanda ya kumadzulo ya Mtsinje wa Troublesome, ndipo ine ndinali kusaka ku mphanda ya kummawa. Ndipo ngati ife tipeza mphalapala, ife timazipachika izo, ndi kudziwa poti tibweretse akavalo odzanyamula, ndipo ife timangokhala pa chishalo cha kavalo wathu.

⁹¹ Ndipo tsiku lina ine ndinali pamwamba kumtunda, ndinatalikirana ndi chishalo changa cha kavalo, ndipo ndinapita kumtunda cha ku malire. Ndipo kumathero kwa kugwa kwa masamba, izo zimatero, chinthu choyambirira inu mukudziwa, dzuwa limawala, kenako nkudzavumba mvula, kenako nkudzayera, kenako nkudzagwa chisanu. Ndipo, basi imangokhala nyengo yosinthasinthu. Ndipo ine ndinali ndikusaka, pamtunda. Kunali kuli kowuma kwenikweni, ndipo ine ndinamva kulira kwa mphenzi; ndipo ndinayang'ana, ikubwera kudutsa mmapiri, ndipo mvula inali ikubwera. Chotero, ine ndinangopita kuseri kwa mtengo ndipo ndinakaima kumeneko kanthawi pang'ono mpaka nkunthowo utatha. Mphepo zimawomba ndi kumavunyuzo, ndi kumazungulira, ndipo ine ndinaima kuseri kwa mitengoyo mpaka izo zonse zitatha. Izo zitatha. . .

⁹² Ine ndinali nditaima pamenepo, ndikuganiza za Mulungu. Izo zangokhala zaka pang'ono zapitazo, ine ndinali ndikuchititsa misonkhano yokopa anthu iyi. Ndipo ine ndinaganiza, "Mulungu ndi wamkulu bwanji, ndiponso wodabwitsa bwanji!" Ine ndinati, "Ine ndiyenera kuti ndinabadwa chifukwa cha malo awa, kuno ku tchire, ndekha ndekha, kutali ndi anthu ndi magulu, ndi odwala ndi osautsika, ndi chirichonse, kulira kwa matelefoni, ndipo ma ambulasi kumabwera." Ine ndinaganiza, "Ndi zokoma bwanji ndi zamtendere! Ambuye, ndiloleni ine ndizikhala kuno. Ndipo ine—ine ndinabadwira ichi, chibadwa changa ndi chimenechi, kuno ndi kumene kuli kwathu. Kuno ndi kumene Inu mumakhala." Ndipo ine ndinaganiza, "Chabwino, ngati ine sindikhala nazo izo kuno, ine ndidzakakhala nazo izo mu Zakachikwi, chotero ine ndingodikirira nthawi imeneyo."

⁹³ Ndipo pamene nkuntho unadzasiya, ine ndinakhala ngati ndinachokako kuseri kwa mtengowo. Ndipo, kutali kumbali ya phiri, ine ndinamva mphalapala yokalamba yamphongo ikuyamba ku—kulira. Ndipo iyo inali kuitana gulu lonse; izo zinali zitabalalika, nthawi ya nkuntho. Ndipo iyo inayamba kuyitana imzake. Kenako monga Davide ananena mu m'Malemba, "Pamene chakuya chiyitanira ku Chakuya"! Ngati

pali chakuya, chikuitanira, pakuyenera kukhala Chakuya kuti chiyankhire kwa icho, kwinakwake.

⁹⁴ Ndiyeno chirengedwe chimenecho chinayamba kuwuka mwa ine. “Awa ndiye malo oti ine ndizikhalako. Oh, imeneyo ndi nyimbo!” Kumbuyo komwe cha kuno, nkhandwe yokalamba yotuwa inakuwa, ndipo imzake inayankha, kumusi pansi. Oh, mai! Pamenepo ndi pamene chakuya chikuitanira kwenikweni ku Chakuya; kumva kuitana kolusa kuja kwa nkhandwe, nyama zina zakuthengo zimafuula, mbalame zimafuula. Kwa ine, ndi Mulungu! Ine ndimakhoza kumumva Iye pakati pa zirombo Zake ndi nyama Zake.

⁹⁵ Mphepo imawomba, ine ndinapezeka ndikuyang’ana mmbuyo kuno kumene a...imawomba, yozizira mokwanira kuumitsa madzi mu zobiriwira. Dzuwa likutuluka, cha kumadzulo, mbali *iyi*, ndipo limawoneka ngati diso likuyang’ana kudutsa kumeneko, ngati Mulungu, mu kulowa kwa dzuwa. Ndipo ine ndinazindikira izo zinapangitsa utawaleza kudutsa pa mpitapo. Ndipo ine ndinayamba kuganiza, “Ndi Ameneyo mu utawaleza. Ndi Uyo apo kutsidya uko, mu kuitana kwa mphalapala iyo. Ndi Uyo apo mwa nkhandwe, akuitana. Ndi Uyu apa ali mmitengo. Ine ndikukhoza kumva liwu Lake likunong’ona. Ndi Uyo apo mu utawaleza.”

⁹⁶ Pakuti, “Iye pomuyang’ana amawoneka ngati mwala wa Yaspi ndi Sardiyo, ndi utawaleza pa mutu Wake; Alfa, Omega, woyamba ndi wotsiriza; Iye amene Anali, Amene Ali, ndipo Ati Adzabwe; Muzu ndi Mphukira ya Davide.” Ndipo ali ndi utawaleza, mitundu seveni, ungwiro. Mulungu amakhala wangwiro mu seveni. Ndipo pamenepo Iye analinso utawaleza, ngati phangano.

⁹⁷ Paliponse pamene inu mungayang’ane, inu mukhoza kumuwona Mulungu, ngati inu mungayang’ane mu chirengedwe Chake. Ndipo pamene ine ndinadzadzidwa...Ndikuuzani inu chinachake, ndikatero inu mudziwa ndine—ndine wa Baptisti weniweni. Pamene ine ndimayang’ana pa zimenezo, ine ndinakhuta kwambiri Mzimu Woyera mpaka kuti ndinayezeka mfuti yanga pa mtengo ndipo ndinathamanga kuzungulira mtengowo mwamphamvu basi mmene ine ndikanathera, ndikuponyera mwendo umodzi mu mlengalenga, ndipo ndikufuula pamwamba pa mawu anga, ndikukuwa, “Aleluya! Aleluya! Aleluya! Aleluya,” basi ndikuzungulira, ndikuzungulira, ndikuzungulira, ndikuzungulira, mpaka ine ndinatsala pang’ono kugwera pansi; kenako ndinaima ndipo ndinagwedeza manja anga mmwamba ndi pansi, ndipo pamenepo ndikukuwa, “Ulemelero! Ulemelero! Ulemelero! Ulemelero! Ulemelero! Aleluya! Aleluya! Aleluya! Aleluya,” basi mwamphamvu mmene ine ndikanathamangira. Ine

sindikanaganizira za china chirichonse choti ndinene. Mtima wanga unali ukubwatamuka.

⁹⁸ Ichu chinali chiyani? Chakuya kuitanira ku Chakuya! Ine ndinamumva Mulungu patali mwanjira imene mwinamwake inu simukanamumva Iye. Koma, kwa ine, Iye anali mu chirengedwe Chake, akuitananso, “Ine ndine Mulungu wa chirengedwe. Ine ndinapanga zinthu zonse ndi dzanja Langa Lomwe.”

⁹⁹ Inde, ngati winawake akanabwera mu nkhalangomo, iwo akanaganiza kuti munali wamisala mnkhalangomo. Ndinali kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira mtengo umenewo, basi ndinali ndikungokhala ndi nthawi ya ulemelero! Ine sindinali...aliyense, ine sindimasamala kaya iwo amandimva, kapena ayi. Ine ndinali mailosi fifite, mailosi sarte, mulimonse, kutalikana ndi aliyense, mmene ine ndimadziwira. Koma ndinazungulira ndi kuzungulira mtengowo ine ndinali, ndikufuula.

¹⁰⁰ Chifukwa chiyani? Ine ndinali mu kachisi wa Mulungu. Ine ndimakhoza kumuwona Iye paliponse, dzuwa, milozo ikudutsa mmitengo, utawaleza uli patali, nkhandwe ikufuula, mphalapala ikufuula. Ine ndimakhoza kumumva Iye mu mphepo. Oh, mai, Iye amapezeka paliponse! Mmwamba mwamba, inu mukanakhoza kuwona kumene chisanu chimawoneka ngati mapiri, ndi kumachitira mthunzi mmusi mobiriwira. Oh, mudzangoyang’ana paliponse, inu mudzamuwona Iye. Iye amakhala mu zammwamba Zake. Inu mukukhulupirira zimenezo? Ine ndinaima pamenepo kwa kanthawi.

¹⁰¹ Ndipo patapita kanthawi ine ndinamva chinachake chikupita, “Chatta, chatta, chatta, chatta! Chatta, chatta, chatta!”

Ine ndinaganiza, “Ndi chiyani chimenecho?”

¹⁰² Ine ndinayang’ana pondizungulira. Panali wogwetsedwera pansu wakale pamenepo pamene a—nkuntho wakale unali utagwetsa mitengo ina, ndipo pamenepo panali gologolo wamng’ono wa mu paini. Ine sindikudziwa ngati inu mukudziwa chimene iwo ali, kapena ayi. Ndi angati amadziwa chimene gologolo wa mu paini ali? Iko ndi kanthu kakang’ono kaphokoso kwambiri kamene kalipo mdziko. Ndipo iye analumphira mmwamba pa chitsa cha mtengo chakale pamenepo. Ndipo basi iye anali akuchita ngati watsala pafupi kuti...iye anali woti andikhadzulira ine mzidutswa, basi, “Chati, chatta, chatta, chatta!” Iye anali akulumpha chokwera-ndi-chotsika, akudzigwedeza paliponse, mwamphamvu mmene akanathera. Oh, iye anali woti andidula ine.

¹⁰³ Chabwino, ine ndinaganiza, “Kanthu kakang’ono, palibe chifukwa choti iwe utengeke chomwecho. Iwe

suchita chirichonse. Ndipo ine, kodi ine, chiyani, kodi ine ndakuwopsyeza iwe?” Ine ndinaganiza, “Chabwino, iwe sukuyenera kuti uchite mantha ndi zimenezo. Ine ndinali kungomupembedza Mulungu amene anatipanga tonsefe.” Mukuona? “Palibe chifukwa choti iwe usokonezeke. Ine ndinali kumupembedza Iye, chotero iwe usatengeke monga choncho. Chabwino, ine ndinali kungomupembedza Mulungu, iwe umayenera kudziwa bwinoko kuposa kuti udzindifuulira ine monga choncho. Usandisokoneze ine pamene ine ndikufuula monga choncho, chifukwa ine ndikukhala ndi nthawi yabwino. Ndisiye ine ndekha.” Mukuona?

¹⁰⁴ Ndipo chotero ine ndinadzazindikira kuti kanthu kakang'onoko kamagwedezera mutu wake chammali, ndipo kamayang'ana pansu mu tchire limenelo. Chabwino, ndinadzapeza kuti iye samandikuwa ine. Kuchokera mu tchire limenelo, kudutsa mu nkunthowo, munali mphungu yaikulu imene inapangitsidwa kutsika pansu. Ndipo inamenyetsedwera pansu mu zimenezo, inawombodwera pansu mu kuwomba uko. Ndipo chinthu chachikulucho, ndicho chimene gologolo wa mpaini wamng'onoyo amatengeka nacho. Ndipo iye analumphira pa nthambi.

¹⁰⁵ Ine ndinaganiza, “Tsopano, dikirani miniti pano, pali chinachake panapake. Chifukwa, ine ndinali kumupembedza Mulungu, ndimathamanga mozungulira ndi kuzungulira mtengo uyu apa. Ndipo ine ndimamuwona Iye mu zipangizo Zake zosiyanasiyana izi, ndi chirengedwe ichi. Tsopano, nchifukwa chiyani kuti Iye wandisokoneza ine chifukwa cha chinthu ngati chimenecho?” Tsopano, pamene pa nali mphungu yokalamba. Ine ndimaisirira mphungu. Koma ine ndinayang'ana pa iyo, ndipo ndinaganiza, “Chabwino, chiyani...Kodi ine ndingamuwone Mulungu mwa iyo? Tsopano kodi chimenecho chingakhale chiyani?”

¹⁰⁶ Ine ndinayang'ana pa iyo. Maso ake aakulu, owoneka motuwa, ndipo iyo inaima pamene pa nthambi iyo, ikundiayang'ana ine. Ndipo inayang'ana pa gologolo uyu, ndipo kenako nkudzayang'ananso pa ine; kenako nkudzayang'ana pa gologolo, kudzayang'ana. Ine ndinati, “Ine ndikuganiza iwe ukutiayang'ana ife.” Chotero ine ndinaganiza, “Kodi iwe ukudziwa chiyani? Ine ndikhoza kukuwombera iwe, ngati ine ndikanafuna.” Ndipo ine ndinayang'ana pa iye. Ndipo mfuti yanga inali itaima motsamira mtengo. Ine ndinati, “Kodi iwe ukudziwa kuti ine ndikhoza kukuwombera iwe ngati ine nditafuna kutero?” Siinapereke chidwi kwa izo, basi inangokhala pamene.

¹⁰⁷ Ine ndinaganiza, “Oh, ndicho chimene Mulungu akufuna kuti ine ndichiwone, ‘Usamawope.’” Mphungu imeneyo ndi yolimba mtima, iyo siimawopa chirichonse. Iyo siingachite

manyazi kumuwuza bwana wake kuti wachiritsidwa ndi machiritso Auzimu. Izo sizingamuvute iye. Iyo—iyo ndi yamphamvu. Iyo siingachite mantha kuti ichitire umboni ngati iyo yalandira Mzimu Woyera. Ngati Iwo unali wa iye, iyo ndithudi ingachitire umboni za Iwo; chifukwa iyo ndi yolimba mtima, palibe choti achite nacho manyazi iye.

¹⁰⁸ “Chabwino,” ine ndinaganiza, “nchiyani chikukulimbitsa mtima iweyo? Nchiyani chikukupangitsa iwe kulimba mtima?” Ine ndinayamba kuzindikira pamenepo, iyo imakhala ikumamverera mapiko amenewo. Inu mukudziwa mmene izo zimasunthira nthenga zake mmbuyo ndi mtsogolo, inu mukudziwa, kukoka mapiko ake. Ine ndinaganiza, “Oh, ine ndawona. Uh-huh. Mulungu anakupatsa iwe mapiko awiri. Ndipo iwe ukudziwa bwino kuti iwe ukhoza kutenga mapiko aakulu awiriwo ndi kupita mu mtengo uwo ine ndisanaifikire nkomwe mfuti imeneyo.” Iyo inali ndi chidaliro ndi chimene. . . Mulungu anamupatsa iye mapiko amenewo, ndipo iye amadziwa chimene mapiko amenewo angamuchitire iye.

¹⁰⁹ Ndi zosiyana bwanji zimenezo ndi munthu! Mulungu anatipatsa ife Mzimu Woyera, ndipo ife sitimadziwabe chimene Iwo ungatichitire ife. Uko nkulondola! Izo ndi zopanda malire, zimene Iye ati adzachite. “Chirichonse chimene inu muchifuna, pamene mupemphera, mukhulupirire kuti mulandira icho, ndipo inu mudzalandira icho.” Mphungu imeneyo imatha kudalira mapiko ake opatsidwa ndi Mulungu. Inu mukudziwa chifukwa chake? Ine ndikuganiza, nthawi zambiri, mphungu yayeserapo zimenezo. Iyo imadziwa chimene iyo ikunena. Ndipo ife tiri nawo Mzimu Woyera ndipo sitinawuyesere Iwo. Apo ndi pamene izo ziri. Mwaona, ngati ife titalola kuti chirengedwe chigwire ntchito mwa ife mmene nyama zimachitira! Ndithudi, iyo imadziwa choti ichigwire, ndi choti isachigwire.

¹¹⁰ Chotero iyo—iyo inadziwa kutalika kuchokera pamene ine ndinali nditaima, kuchokera pa mfuti yanga, iyo ikanakhala ili mu mtengo umenewo ndipo ine sindikanaiwonanso iyo nkomwe, chotero iyo inakhala ikukupiza mapiko aakulu amenewo. Ndipo ine ndimaiyang’ana iyo, ine ndinati, “Mnyamata wokalamba, ine sindingakuwombere iwe nkomwe. Ine ndikukunyadira iwe!” Ine ndimakonda kuwona chinachake chimene chiri ndi kulimba mtima kwa icho, chinachake chimene chingaimirire pamene iwo akudziwa chimene iwo akuchita. Kodi inu simumakonda kuwona zimenezo?

¹¹¹ Ndi chifukwa chake ine ndimakonda mpingo wa Pentekoste. Sumasamala kaya dziko likunena chiyani, kuwatchula iwo “oyera odzigudubuza,” china chirichonse, iwo amaaimirirabe ndi kufuula chimodzimodzi, kutamanda Ambuye, kumapitirirabe. Ine ndimazikonda zimenezo. Ndithudi, kuima ndi zimenezo. Sizimapanga kusiyana kulikonse kuti ndi ndani, mukhale

pamenepo ndipo mupereke umboni wanu, mumupatse Mulungu matamando.

¹¹² Ine ndinaiwona mphungu yokalamba iyi pamene iyo imazungulira pamenepo, inu mukudziwa, pang'ono chabe. Ndipo ine ndinapezeka ndikuzindikira, iyo sikuti imandiyang'ana ine kwambiri, iyo imatopa ndi kumamvetsera gologolo uyo akumunyoza iye, "Chatta, chatta, chatta! Chatta, chatta, chatta!" Ah, iyo imangoyang'ana pa iye. Ndipo patadutsa kanthawi iyo inakwiya naye, chotero, chinthu chokhacho chimene iyo inachita chinali kungopanga kudumpha kwakukulu monga *choncho*, ndipo inakupiza mapiko ake pafupifupi kawiri, ndipo iyo inali pamwamba pa mitengo. Kenako iyo siinakupizenso kenanso, iyo inangokhazika mapiko ake. Ndipo nthawi iliyonse mphepo ikakwera, iyo imakwera nayo iyo. Ndipo ine ndinaima pamenepo ndipo ndimayang'ana pa iyo. Pakuti nthawi iliyonse mphepo ikawomba, iyo imapita mmwamba pang'ono; osasuntha nthenga nkomwe, basi kumangopita mmwamba, mmwamba, mmwamba, mmwamba, mpaka iyo inadzasanduka kadontho kakang'ono.

¹¹³ Ine ndinaima pamenepo, ndipo misonzi inayamba kutsikira mmasaya anga. Ine ndinati, "O Mulungu, awa ndi malo opambana kukhalapo. Kuno ndi kumene ine ndimakonda kukhalako. Ndinu muli apo mu mphungu imeneyo.

¹¹⁴ Mwaona, iyo inangopanga kudumpha kumodzi kwakukulu, ndipo iyo imadalira mapiko akewo. Iyo siimadumpha kuchokera pa msonkhano umodzi kupita kwa wina, ndi kupita kuchoka pa mpingo umodzi kupita pa wina. Iyo inangopanga kudumpha kumodzi kwakukulu, kenako inadzakhazika mapiko ake mu Mphamvu ya Mulungu, kuwulola Mzimu Woyera, kuti umutengere iye kutali, kumapita ndi kumapita, ndi kumapita ndi kumapita. Iyo inachoka kwa agologolo aang'ono akale awa apa dziko kuno, okhazikika padziko; opanda mapiko, ndipo osadziwa kuuluka. "Chatta, chatta! Masiku a zozizwitsa anapita. Palibepo chinthu chotere ngati Mzimu Woyera, zimenezo ndi za tsiku lina limene linadutsa." Oh, ingokhazikani mapiko anu mu Mphamvu ya Mulungu, mulole Mzimu Woyera ukunyamulireni inu pamwamba pa izo, kazipitirirani ndi kumapita ndi kumapita. Iyo sinkamumvanso nkomwe gologolo, gologolo wa mdothi, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kumutchula iye. Inatopa ndi "chatta, chatta." Oh, ngati mpingo, limodzi la masiku awa, udzatope ndi zimenezo, ndipo iwo nkudzadziwa mmene angakhazikire mapiko awo; ndipo nkudzayenda ndi Mulungu, ndi kumapita Kwawo, kuchoka kwa izo. "Masiku a zozizwitsa anapita"? Ndiuzeni ine kuti ndi liti. Angobwera mochedwa kudzatiuza ife zimenezo, sichoncho iwo? "Masiku a zozizwitsa anapita. Palibepo chinthu chotero ngati Mzimu Woyera. Kuyankhula mmalirime ndi zongodzipangitsa kukhulupirira," ndizo zonse zimene iwo amadziwa za izo.

Chotero, chinthu choyenera kuchita ndi kungokhazika mapiko anu.

¹¹⁵ Iyo siimakupiza, tsopano, malo ndi malo. “Ine ndipita uko ndipo ndikawone ngati *ichi*, ndipo ine ndipitako ndipo ndikawona ngati *icho*.” Iyo inangodziwa mmene ingakhazikire mapiko ake. Ndipo ndizo zonse zimene inu mukuyenera kudziwa mmene mungachitire ndi Machiritso Auzimu, zokhudza Mzimu Woyera, ndi kungodziwa mmene mungaikire chikhulupiriro chanu mu mphamvu ndi malonjezo a Mulungu. Iwo udzakunyamulirani inu mmwamba. Inu muzingopita mmwamba. Nthawi iliyonse imene iyo iwomba, ife tidzakwera mmwamba ndi mmwamba, ndi mmwamba ndi mmwamba; mpaka inu simudzatha kumva izi apa, “Chatta, chatta, chatta! Masiku a zozizwitsa anapita. Gulu la oyera odzigudubuza.” Inu simudzalabadira nkomwe zimenezo. Inu mudzapita kutali kudutsa zimenezo mpaka inu mudzakakhala koti simukuzimvanso izo. Solo yanu idzanyamuliridwira kufika pamalo amene. . .

¹¹⁶ Oh, ndithudi, Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake. Inu mukukhulupirira zimenezo, sichoncho inu? Oh, ife tikhoza kukhala maora basi pa chinthu chimodzi chimenecho. Ife tikuyenera tilumphire kwa china. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake? Tsopano, chotsatira, Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Tsopano inu mukayang’ana pa chirengedwe ndipo mudzamuwona Mulungu. Ndithudi, inu mudzatero. Tsopano Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake.

¹¹⁷ Tsopano, Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Mulungu amasunga Mawu Ake. Zimenezo ndi zimene zimapangitsa Baibulo kukhala lenileni. Ndicho chimene ife tingamutsutsire wachikunja aliyense, wosakhulupirira aliyense, wa Chimuhamadi aliyense, wa Chibuddha aliyense, msing’anga aliyense, wazauzimu aliyense, china chirichonse, mu Dzina la Ambuye Yesu, ndi kuwapanga Mawu awa kukhala amoyo, chifukwa Mulungu amakhala mu Mawu Ake.

¹¹⁸ Ine ndinali kukambirana, tsiku lina, ndi a—mpingo wina wa chipembedzo umene umakhulupirira kuti—kuti mpingo ndiwo yankho, osati Mawu. Iwo amati iwo analemba Baibulo. Baibulo linali . . . ilo linali mbiriyakale ya mpingo wawo. Ndipo iye anati, “Mulungu amakhala mu mpingo Wake.”

Ine ndinati, “Baibulo linati, ‘Mulungu amakhala mu Mawu Ake.’”

¹¹⁹ “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Uko nkulondola. Iye anali Mawu a Mulungu, Mawu oyankhulidwa a Mulungu. Ndipo Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Lonjezo lirilonse

limene Mulungu amapanga, Iye amaima ndi lonjezo Lake. Chinthu chokhacho chimene ife tikuyenera kuchita, ndicho, ife tizitengera Mawu Ake mu mtima mwathu, ndipo tisamawakaikire Iwo, koma tiziwakhulupirira, tikatero Mulungu adzapanga Mawu amenewo (amene ali Iyemwini mkati mwa inu) kupita kukagwira ntchito ndi kukwaniritsa chinthu chomwecho chimene Iye analonjeza.

¹²⁰ Kodi Iye anachita izo mwa Abrahamu? Bwanji, Abrahamu, bambo wa usinkhu wa zaka sikisite faifi, kapena, iye asanati nkomwe, kapena, usinkhu wa zaka sevente faifi, iye asanalandire lonjezo. Ndipo iye anatengera Mawu amenewo mu mtima mwake ndipo anawasunga Iwo mmenemo kwa zaka twente faifi. Koma iwo anabereka ndendende chimene lonjezo linali. Kodi uko nkulondola?

¹²¹ Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Ife tonse timadziwa zimenezo. Palibepo kachidutswa kamodzi ka Baibulo kamene kamadzitsutsa Kokha. Ine ndamubetcherapo aliyense chirichonse chimene iwo akuchifuna; ine ndidzalalikira Uthenga ndi kutenga chopereka chachikondi kwa chaka, ndi kuchipereka icho, chirichonse, kwa munthu amene angatenge Mawu a Mulungu ndi kuwatsutsa Iwo mwa Mawu a Mulungu, kwa ine. Uko nkulondola. Izo mulibemo mmenemo. Ndipo ine ndakhalapo nako kubetchera kumeneko kwa zaka ndi zaka; ine ndikutengabe zopereka zanga zachikondi. Chifukwa, izo mulibemo mmenemo. Inu mukhoza kukhala wokhazikika kwambiri mu za luntha zanu, chifukwa Baibulo ndi... Yesu anawathokoza Atate Ake chifukwa “chobisa Izo mmaso a anzeru ndi aluntha, ndi kuziulula Izo kwa makanda amene angaphunzire.” Mwaona, Iwo ndi Mawu a Mulungu.

Mawu ali ngati Mbewu.

¹²² Tsopano, inu mutenge mbewu. Anthu inu kuno a ku Gombe Lakumadzulo, inu ndi alimi opambana. Tsopano, mutenge mtengo wanu wa malalanje. Tsopano, inu mutenge mtengo wanu wa malalanje, pamene muwutenga iwo koyamba, iwo umakhala njere. Inu mukaiyika iyo mu nthaka, ndipo njere imeneyo idzabala mtengo wa malalanje. Ndithudi. Tsopano, umo ndi mmene izo zimakhallira. Tsopano, mtengo wa lalanje uwu, chinthu chokhacho chimene inu mungachite ndi iwo, pamene iwo watalika ngati wanu... kotalika inchi imodzi. Ine sindikudziwa kuti ndi madengu amalalanje angati amene mtengo ungabereke pa moyo wake. Tiyeni tinene, mwa chitsanzo, madengu faifi handiredi. Tsopano, zimenezo zikhoza kukhala zopitirira kapena zocheperapo, ine sindikudziwa; koma tinene kuti madengu faifi handirendi. Kodi inu mumadziwa kuti lalanje lirilonse limene lidzakhale konse mu mtengo umenewo linali mmenemo pamene iwo unangokhala utali wa inchi imodzi? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Kodi inu

mumadziwa zimenezo? Ndithudi, izo ziri. Kuti? Izo zinachokera ku njereyo. Tsopano, chinthu chokhacho chimene icho chiri, iyo inangodalidwa, inayambitsidwa.

¹²³ Ndipo iwo umayenera kukoka, iwo umayamwa madzi kuchokera mu nthaka, kuti uzipeza chakudya. Ndipo iwo umayamwa madzi kuchokera mu nthaka, ndipo iwo umayenera uzimwa kuposa gawo lake. Ndipo nthawi iliyonse . . . chifukwa, iwo umayenera udzitulutsa panja. Ndipo pamene iwo ukumwa madzi, iwo umatulutsa nthambi; ukamwa madzi ambiri, umatulutsa masamba; ukamwa madzi ambiri, umatulutsa panja masamba; ukamamwa madzi ambiri, umakankhira panja malalanje. Iwo umangokhalira kumwa, ndi kumatulutsa panja. Koma, iwo umayenera uzimwa.

¹²⁴ Umo ndi mmene wokhulupirira aliri, iye amakhazikidwa pakati pomwe pa Mawu a Mulungu. Ameni! Ndipo ngati iye ali ndi chosowa chirichonse, iye amangomwa, ndi kutulutsa panja; kumwa, ndi kutulutsa panja. Pamene munthu wadzazidwa ndi Mzimu Woyera, chirichonse chimene iye ati adzachigwiritse konse ntchito mu ulendo wake wa moyo chimakhala mwa iye pomwepo. Inde, bwana. Chinthu chokhacho chimene ife tikuyenera kuchita ndi kumwa ndi kumwa, ndi kumwa ndi kumwa, ndi kumwa mpaka ife titachipeza icho. Ife tinabzalidwa mwa Khristu Yesu! Ndipo kutanthauzira kwanga kwa Iye, Iye ndi Kasupe wa Moyo wosatha. Ndipo ndendende chimene ine ndikuganiza kuti Iye ali. Ndipo pamene ife tabzalidwa mwa Iye, Iye ndi wosatha! Ife tikhoza kutunga kuchokera kwa Iye, ubwino, kufatsa, unjonda, chipiriro, mphamvu, machiritso, [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. . . lonjezo limene Iye anapereka, chifukwa ife tabzalidwa mu Mbewu ya Mawu Ake. Ndipo Iyo idzabereka ndendende basi chimene Mulungu ananena kuti Iyo idzabereka. Iyo ndi Mbewu, Mawu.

¹²⁵ Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Ife timakhulupirira zimenezo, sichoncho ife? Tonse a ife timakhulupirira. Inu mukumuwona Mulungu akuyankha. Zaka zakutali zapitazo, pamene Iye anawauza iwo kuti azipita uko, ku Pentekoste, iwo akalandira Mzimu Woyera. Zaka izo zisanachitike, mu Yesaya, Iye anati, “Langizo likuyenera kukhala pa langizo, mzere pa mzere, apa pang’ono ndi apo pang’ono. Gwiritsitsani icho chimene chiri chabwino. Milomo yachibwibwi ndi malirime ena Ine ndidzayankhula ndi anthu awa, ndipo uwu ndi Mpumulo.” Mwaona, Iye anazinena izo mmbuyo, kenako Mawu Ake anadzabwera ndipo anadzawonetseredwa. Zonse, Mesiya wolonjezedwa, kuchokera mmunda wa Edeni, “Mbewu ikuyenera ivulaze mutu wa serpenti,” zina zotero, zinakwaniritsidwa. Mulungu amakhala mu Mawu Ake.

¹²⁶ Tsopano, Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake, nenani “ameni” ngati inu mukukhulupirira izo.

[Osonkhana akuti, “Ameni”—Mkonzi]. Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Inu mukukhulupirira zimenezo, nenani “ameni.” [“Ameni”]

¹²⁷ Tsopano, Mulungu mwa Mwana Wake. Tsopano, Mulungu anali mwa Mwana Wake. “Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjaniitsa dziko kwa Iyemwini,” icho ndi chimene Lemba limanena. Iye, Mulungu adzatsika pansi, ndipo anadzakhala mu thupi, lobadwa mwa namwali Maria, ndipo Mulungu anadziwonetsera Yekha kudzera mwa Khristu; kuti adzawonetsere kuti Zake—zikhumbo Zake zinali, kuti adzawonetsere kuti Iye anakonda, kuti adzawonetsere chipiriro Chake, kuti adzawonetsere mphamvu Yake, kuti adzawonetsere ndi kudziwonetsera Yekha. Mulungu ankakhala mwa Khristu, akuliyanjaniitsa dziko kwa Iyemwini.

¹²⁸ Ine ndimayankhula ndi mkazi, kuno nthawi ina kale, kapena iye anaitanira tcheru changa. Iye anati, “Abusa Branham,” iye anati, “Ine ndimayamikira maulaliki anu. Ine, ndine a . . . Ine ndimakhala pa misonkhano yanu.” Koma iye anali wa mpingo wa chipembedzo chinachake umene sumakhulupirira kuti Yesu anali Waumulungu. Ndipo iye anati, “Chabwino, Iye sanali Waumulungu.” Ndipo ine ndinati. . . Anati, “Inu mumayetsa kumupanga Iye Waumulungu kwambiri.”

Ine ndinati, “Iye anali Waumulungu.”

¹²⁹ “Oh,” iye anati, “bwana, ine ndingavomereze kuti Iye anali munthu wabwino.” Ndipo ine sindikufuna kuti ndivulaze kumverera kwanu; ena a anthu amenewo ndi azimzanga ofunika. Iyo ndi Sayansi ya Chikhristu. Ndipo iye anati, “Iye, Iye si Waumulungu.” Anati, “Ine ndingavomereze kuti Iye anali mneneri, koma Iye sanali Waumulungu. Ndipo inu mumayetsa kumupanga Iye Waumulungu.”

¹³⁰ Ine ndinati, “Iye mwina anali Waumulungu kapena wachinyengo wamkulu amene dziko linayamba lakhalapo naye.” Uko nkulondola. Ine ndinati, “Iye anali Waumulungu. Iye anali woposa mneneri. Iye anali Mulungu pamwamba pa aneneri! Ndithudi, Iye anali.” Ine ndinati, “Iye anali Waumulungu.”

¹³¹ Ndipo iye anati, “Tsopano, inu munati inu ndinu ‘wachikhazikitso,’ ndipo mumakhulupirira Lemba.”

Ine ndinati, “Ine ndimatero.”

¹³² Ndipo iye anati, “Ngati ine nditatsimikizira kwa inu, mwa Baibulo lanu lomwe, kuti Iye sanali Waumulungu, kodi inu mungachitire umboni kuti ine ndikulondola?”

¹³³ Ine ndinati, “Inde, bwana. Ngati Baibulo litanena kuti Iye sanali Waumulungu, ndiye ine ndikhulupirira Baibulo.” Ndipo ine ndinati, “Koma ine ndikuyenera ndiwone Malemba.”

¹³⁴ Iye anati, “Mu Yohane, cha mu Yohane Woyera, Iwo amati, ‘Pamene Yesu anapita ku manda a Lazaro, Iye analira.’” Ndipo

anati, “Inu mukudziwa, ngati Iye anali Waumulungu, Iye sakanalira.”

Ine ndinati, “Mlongo, kodi apo ndi pamene inu mukukhazikitsapo lingaliro lanu?”

¹³⁵ Iye anati, “Inde, bwana. Ndipo izo nzoona. Iye anapita ku manda a Lazaro, Iye analira; zimenezo zinawonetsera kuti Iye sanali Waumulungu.”

¹³⁶ Ine ndinati, “Mtsutso wanuwo ndi wopyapyala kuposa nsuzi wopangidwa kuchokera ku mthunzi wa nkhuu yakufa ndi njala.” Ine ndinati, “Chabwino, inu mukudziwa bwinoko kuposa zimenezo.”

¹³⁷ Ndipo iye anati, “Oh, Iye anali—Iye anali—Iye anali mneneri, Iye anali munthu wabwino.”

¹³⁸ Ine ndinati, “Iye anali woposa. . . Mulungu amakhala mwa Iye. Iye anali munthu, koma Iye anali a—Munthu wa pawiri. Mmodzi, Iye anali munthu; Mzimu mwa Iye unali Mulungu!” Ine ndinati, “Mulungu amakhala mwa Khristu.”

Iye anati, “Ah! Ayi!”

¹³⁹ Ine ndinati, “Taonani, dona, ine nditenga Lemba lanu lomwe. Iye anali munthu, koma Iye anali Mulungu-munthu. Pamene Iye anapita ku manda a Lazaro, Iye analira ngati munthu. Izo nzoona. Koma pamene Iye anaima pamene, nawongola mapewa Ake aang’ono akugwa, ndipo nkudzati, ‘Lazaro, dzuka,’ ndipo munthu wakufa, amene anali atafa kwa masiku anayi, anabwerera ku moyo, ameneyo anali woposa munthu. Munthu sakanachita zimenezo. Ameneyo anali Mulungu mwa Mwana Wake.”

¹⁴⁰ Iye anali munthu pamene Iye ankatsika ku phiri, ali ndi njala, akufunafuna chinachake choti adye, akuyang’ana pa mtengo kuti apeze chinachake choti adye. Iye anali munthu pamene Iye anali ndi njala. Koma pamene Iye anatenga nsomba ziwiri ndi mabisiketi asanu ndi kudyetisa faifi sauzande ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu mwa Mwana Wake. Ndithudi anali!

¹⁴¹ Iye anali munthu pamene Iye anali atagona kujaku pa ngalawa ija usiku umenewo, ukoma unali utamuchokera Iye, mpaka Iye anali wofooka kwambiri Iye sakanati. . . mafunde sanamudzutse Iye nkomwe, akusunthidwa sunthidwa mu ngalawa yaing’ono yakale iyo, ngati chivinikiro cha botolo kunja uko pa nyanja yamphamvu. Ziwanda teni sauzande za mnyanja zinalumbira kuti zimumiza Iye usiku umenewo pamene Iye anali akugona. Iye anali munthu pamene Iye anali ndi tulo ndipo atatopa. Koma pamene Iye anadzaika phazi Lake mmphetepe mwa ngalawayo, anayang’ana mmwamba ndipo anati, “Mtendere, pakhale bata,” ndipo mphepo ndi mafunde

zinamumvera Iye, ameneyo anali woposa munthu. Mulungu anali ali mwa Mwana Wake! Ndithudi!

142 Iye anali munthu pamene Iye anafa uko pa mtanda, akufuulira chifundo. Iye anali munthu pamene Iye anafa. Iye analira ngati munthu, Iye anali ndi ululu ngati munthu. Koma mmawa wa Isitara pamene Iye anadzamatula a . . . imfa, gehena, ndi zomatira za manda, ndi kuuka kachiwiri; Iye ndi woposa munthu, Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mulungu!

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa,
Iye anandipulumutsa ine;
Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
anga kutali;
Powuka, iye anandilungamitsa mwaulele
kwanthawizonse;
Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku
laulemerero!

143 Mulungu amakhala mwa Mwana Wake, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndithudi. Mulungu amakhala mwa Mwana Wake. Mwamsanga, nthawi yathu ikutha. Chinthu china chowonjezera. Ife . . . Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake? Mulungu amakhala mu Mawu Ake? Mulungu anali mwa Mwana Wake?

144 Tsopano, Mulungu mwa anthu Ake. Chabwino. Ife tiwona ngati Iye amatsika kubwera mwa anthu chimodzimodzi monga Iye amachitira kwa chirengedwe. Anthu ndi gawo la chirengedwe Chake. Ndithudi, iwo ali. Tsopano, zindikirani, Mulungu amakhala mwa anthu Ake.

145 Anali ndani usiku wina uja mu phunziro lathu, mwa Eliya, pamene khanda laling'ono linafa chifukwa chowombedwa ndi dzuwa, ndipo anali ataikidwa kwa maora ndi maora pa bedi ya mneneri, pamene munthu, wotchedwa "Eliya," anayendayenda mmbuyo ndi mtsogolo, chokwera ndi chotsika pansipo, ndipo anadzaligoneka thupi lake pa khanda lakufa ilo, ndipo iye anadzabwerera ku moyo? Ameneyo anali Mulungu mwa anthu Ake. Izo ndithudi zinali.

146 Anali ndani iye, kuti pamene Petro Woyera, mtumwi, nsodzi mbuli kwambiri . . . Baibulo linati, "Iye anali mbuli ndi wosaphunzira." Anali ndani, pamene iye ankayenda pansi mmisewu, ndipo anthu nkumaika odwala mu mthunzi wa munthu ameneyo, ndipo iwo nkumachiritsidwa? Kodi unali mthunzi wa munthu umene unkawachiritsa iwo? Anali Mulungu mwa anthu Ake, amene ankachita kuchiritsako.

147 Anali ndani mwa Paulo Woyera, pamene iwo ankatenga kuchokera pathupi lake mipango ndi zovala, ndi kukaziika pa odwala? Mulungu amakhala mwa anthu Ake. Iwo

anamuzindikira Mulungu mwa Paulo Woyera. Ndithudi, iwo anatero.

¹⁴⁸ Anali ndani pamene gulu la amantha laling'ono linapemphera, linatenga Mawu a Mulungu ndi kupita ku Pentekoste? Iwo anatseka zitseko zonse, ndipo mazenera anatsekedwa, ndipo iwo anakhala mmenemo kwa masiku teni. Mwadzidzidzi panadzabwera phokoso kuchokera Kumwamba ngati mphepo yankuntho, yamphamvu, iyo inadzadza nyumba yonse pamene iwo anali atakhala, malirime ogawanikana ataikidwa pa iwo, ngati moto. Ndipo anatuluka kupita mmisewu, kumene iwo nthawi yina ankawopako, anapita kumeneko, akulalikira Uthenga ndi kumapitirira ngati gulu la anthu oledzera. Icho chinali chiyani? Mulungu ali mwa anthu Ake. Mulungu akuyenda pakati pa anthu Ake.

¹⁴⁹ Mulungu ali mwa inu. Mulungu, Mzimu Woyera, akukhala mwa inu, akuyenda yenda tsopano, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini.

¹⁵⁰ Nchiyani chimawapangitsa atumiki odzozedwa awa kulalikira Uthenga? Nchiyani chimawapangitsa iwo? Mwinamwake, nthawi ina, anali oledzera; nthawi ina, anali anjuga; nthawi ina, anali munthu woyipa; mwadzidzidzi, chinachake chinasinthika! Ndipo apa iwo ayima, akulalikira Uthenga ndipo akupereka miyoyo yawo. Ndipo ena a iwo, pafupifupi, akukhala osauka mmene iwo akanakhalira. Pamene iwo akadakhala amuna amalonda ndipo akanatha kulemera, kumakwera magalimoto aakulu ndi kumakhala mwawofuwofu, koma iwo anapereka nsembe zimenezo ndipo anapereka izo. Bwanji? Mulungu amakhala mwa anthu Ake, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Mulungu akukhala mwa anthu Ake.

¹⁵¹ Ndi chiyani chimene chimamukhudza mkazi wamng'ono kapena mwamuna wamng'ono, ndipo iye nkudzukapo, ndipo nkhope yake nkuwala ngati kandulo, ndipo nkuyankhula chinenero chimene iye sakuchidziwa nkomwe, ndipo wina nkudzuka pansu pa kudzoda komweko ndi kudzapereka uthenga kwa mpingo? Mulungu mwa anthu Ake. Amen.

¹⁵² Nchiyani chimene chimabwera pa nsanja iyi, msonkhano pambuyo pa msonkhano, nkudzachita zozizwitsa zomwezo zimene Yesu anachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi? Ndi Mulungu mwa anthu Ake. Ziribe kanthu ndi mochuluka bwanji mmene chingakhalire mwa ine, icho chikuyenera kukhala mwa inu, nanunso. Chifukwa, icho sichingagwire ntchito mwa ine ndekha. Izo zimatengera inu ndi ine pamodzi, kuti tikachite izo. Uko nkulondola.

¹⁵³ Tonse a ife pamodzi, Mulungu mwa ife tonse! Mulungu, osati kokha mwa Amethodisti kapena Abaptisti, kapena Apentekoste kapena Apresbateria, koma Mulungu akukhala mwa wokhulupirira aliyense amene walandira Mzimu

Woyera. Ameneyo ndi Mulungu, Mzimu Woyera, mwa anthu, akuyanjanitsa dziko kwa Iyemwini.

¹⁵⁴ Taonani momwe Iye amawapangitsira anthu kukhulupirira izi. Mwa zinthu zomwezo zimene Iye anachita kwa oyambirira aja pa Pentekoste, Iye akuchita izo kwa iwo lero, mwanjira yomweyo. Iwo analandira Mzimu Woyera mwa kachitidwe komweko, zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa zikuwatsatira iwo.

¹⁵⁵ Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Mulungu akukhala mwa Mwana Wake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Mulungu akukhala mwa anthu Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Mulungu akuyenda mwa onse!

¹⁵⁶ Chotero Filipo anati, “Tiwonetseni ife Atate, ndipo chitikwanira ife.”

¹⁵⁷ Ndine wokhutitsidwa lero kuti ndikukhoza kumuwona Mulungu paliponse pamene ine ndikuyang’ana! Ine sindikungomuwona Iye, koma ine ndikumumverera Iye ndipo ine ndikudziwa kuti Iye ali pano! Monga wandakatulo ananenera, “Inu mukundifunsa ine mmene ine ndikudziwira kuti Iye ali moyo, Iye akukhala moyo mu mtima mwanga.” Ine ndimawona Mzimu Wake ndipo ndimawuwona Iwo ukundikondoweza ine, ukundisuntha ine. Inu mumakondowedwa ndi Chinachake, Mzimu Woyera. Mulungu ali pano lero, abwenzi. Mulungu ali pano.

¹⁵⁸ Iye amakhala mu chirengedwe Chake kunja uko, mchirimwe ndi mchisanu, masamba, maluwa, mbalame, nyama. Iye amakhala mu kulowa kwa dzuwa, nkutuluka kwa dzuwa. Iye amakhala mu zowunikira zammwamba. Iye amakhala paliponse! Mulungu amakhala paliponse! Iye amakhala mu chirengedwe Chake.

¹⁵⁹ Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Aliyense akatenga Mawu Ake, lonjezo lililonse. . .Ndiloreni ine ndijambulidwe ponena izi. Ngati inu mungatenge lingaliro labwino pa lonjezo Laumulungu lililonse la Mulungu, ilo lidzapangitsa izo kukwaniritsika. Izo ndi zimene ine ndimaganiza za Mawu Ake. Inu mukatenga lonjezo lililonse Apa, ndipo inu nkukhala lingaliro loyenera pa izo, Mulungu adzadzizapangitsa izo kukwaniritsika chifukwa cha inu. Mulungu amakhala mu Mawu Ake.

¹⁶⁰ Mulungu amakhala mwa Mwana Wake. Iye anali Waumulungu. Iye ndi Mwana wa Mulungu. Ine ndimakhulupirira zimenezo ndi zonse zimene ziri mwa ine. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Inde, bwana. Iye sanali woposa. . . Iye anali mneneri. Ndithudi, Iye anali mneneri, Iye anali mlaliki,

Iye anali woyimba. Iye anali—Iye anali Mulungu, Mulungu anawonetseredwa mu thupi. Mulungu anatsika pansu mu thupi, kuti adzaliyanjanitse dziko kwa Iyemwini. Kenako Mwana wodabwitsa wa Mulungu uja anafa. Ndipo, pamene Iye anafa, Iye anapereka moyo Wake. Iye anaukansa pa Isitara, ndipo Mulungu anadzutsa thupi Lake ndipo anadzalikhazika ilo kumbali Yake ya kumanja, ndipo anatumiza Mzimu Woyera kuti udzapitirize kudziwonetsera Iyemwini pakati pa anthu.

¹⁶¹ Ndipo Mzimu womwewo umene umakhala mwa Yesu Khristu uli pakati pathu lero, kudziwonetsera Iwoeni mopitirira kwa anthu, mwa zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, kuwapatsa iwo Mzimu Woyera womwewo, kumayankhula ndi mtundu womwewo wa malirime, kumapereka mtundu womwewo wa kutanthauzira, kumawona masomphenya, kumasunthasuntha, kuchiritsa odwala, basi ndendende monga Iye ankachitira pachiyambi. Mulungu amakhala mwa anthu Ake!

¹⁶² Nchifukwa chiyani timafunafuna ndiye, “Tiwonetseni ife Atate ndipo zitikwanira ife”? Ife tikuwawona Atate. Ife tikuwawona Atate.

¹⁶³ Pamene ine—pamene ine ndiyang’ana kunja kuno ndipo nkuwona dzuwa likulowa, ine ndimawawona Atate. Pamene ine ndiwona dzuwa likutuluka, ine ndimawawona Atate. Pamene ine ndimva kuyitana kwakutchire kwa nyama, ine ndimawawona Atate. Pamene ine ndiwona maluwa amenewo akuphukira, ine ndimawawona Atate. Sichoncho inu?

¹⁶⁴ Ine ndimawawona Iye mu Mawu Ake. Nthawi iliyonse imene nditengera Mawu Ake ku lonjezo, ine ndimawawona Atate.

¹⁶⁵ Ine ndimayang’ana pa Yesu, ine ndimawawona Atate akudzifotokoza Wokha kudzera mwa Mwana.

¹⁶⁶ Ine ndikayang’ana pa anthu Ake, ine ndimawawona Atate; ndimawawona Iye akugwira ntchito pakati pa anthu Ake, akudzifotokoza Iyemwini, kumapitirirabe. “Ndiwonetseni ine Atate”? Ndi Uyu apa pomwe apa masana ano, akugwira ntchito pakati pa anthu Ake, mwa anthu Ake, kudzera mwa anthu Ake, pa anthu Ake. Aleluya! Mulungu ali mwa anthu Ake.

¹⁶⁷ Tiyeni tipemphere. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Matamando akhale kwa Mulungu! Kodi inu mumamukonda Iye? Chabwino.

¹⁶⁸ Ine ndikukhulupirira Billy anandiuza ine a pemphero fifite. . . Chabwino. Khadi la pemphero nambala wani. Kwezani mmwamba dzanja lanu, mwachangu, kuti tithe kuwona tsopano, ndipo mubwere mwamsanga pa mzere wa pemphero. Ife tiwona chinachake chikuchitika. Ine. . . Kodi inu mukudikirira icho? Khadi la pemphero nambala wani, ndani ali nalo? Dona uyu apa, inu muli ndi khadi la pemphero nambala wani? Ine ndikufunsa

khadi la pemphero nambala wani. (Chiyani—linali chilembo chanji?) E.

169 Khadi la pemphero E, nambala wani, kwezani mmwamba dzanja lanu. Nambala thuu. Chabwino. Nambala firii, nambala foro. Bwerani konkuno, mutero inu? Nambala faifi, sikisi, seveni. Uko nkulondola, dzukani. Basi pamene ine ndikuitana, imirirani. Seveni, eyiti, naini, teni, leveni, thwelofu, sartini, fortini, fifitini, sikisitini, seventini, eyitini, naintini, twente, twente-wani, twente-thuu, twente-firii, twente-foro, twente-faifi, mungokhala pa mzere tsopano.

170 Ndi angati amene alibe khadi la pemphero, kwezani mmwamba dzanja lanu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amakhala mwa anthu Ake? Mulungu yemwe uja amene ankayenda mu Galileya, mwa Yesu Khristu, kodi inu mukukhulupirira Iye ali pano lero, mwa inu, Mzimu womwewo umene unali mwa Yesu? Iye ndi Mwana wa Mulungu wobadwa mwa namwali; ndipo ndinu ana okhazikitsidwa, ndi Iye. Mzimu womwewo umene unali mwa Iye, uli mwa inu. Chabwino.

171 Twente-faifi, twente-sikisi, twente-seveni, twente-eyiti, twente-naini, sate, aloleni amenewo abwere. Ife timawaitana iwo monga chomwecho kuti tisadzadzane, inu mukudziwa, zoyendayenda kwambiri. Chabwino, sate, sate-wani, sate-thuu, sate-firii, sate-foro, sate-faifi, sate-sikisi, sate-seveni, sate-eyiti, sate-naini, forte. Uko nkulondola, mungosunthira mmusi kumeneko ndipo iwo akuikani inu mu mzere. Ngati inu simungathe kuyenda, bwanji, mumudziwitse wina, iwo adzakunyamulani inu.

172 Tsopano, ndi angati amene alibe khadi la pemphero, kwezani mmwamba dzanja lanu, munene, “Ine ndikufuna Mulungu kuti andichiritse ine masana ano.” Ine sindikusamala kuti ndinu ndani, kumene mukuchokera, chirichonse, mungoti, “Ine ndikufuna kuti Mulungu andichiritse ine. Ine ndikukhulupirira.”

173 Chabwino, forte mpaka fifite tsopano, aloleni iwo abwere. Aliyense amene ali ndi khadi la pemphero, dzukani ndipo mubwere kuno tsopano, inu amene muli ndi khadi la pemphero lanu. Ife tingodikirira mphindi pang’ono ndipo tiyambira pa mzere, kupempherera odwala.

174 Tsopano, ife tiyenera kuti tikhale titamaliza mu maminiti teni kapena fifitini otsatirawa, chotero mupirire nafe pang’ono. Ndipo mupemphere ndi zonse zimene ziri mwa inu. Tsopano ine ndikufuna kuti inu muyang’ane mbali iyi, aliyense wa inu tsopano. Tsopano kumbukirani. . .

175 Kodi alipo alendo aliwonse pano amene sanakhalepo mu umodzi wa misonkhano? Alipo ochepa chabe, tangowonani. Ndife okondwa kwambiri kukhala nanu. Tikudalira kuti inu

mutero—mupitirira ndi mtundu uwu wa msonkhano, uko ndikuti, kumene Mzimu Woyera... Ngati inu sindinu a—membala wa mpingo wina umene uli wa Uthenga wathunthu, ndipo mwa chibadwa, ife tingakufunsemi inu, ngati inu mmakonda mtundu wa msonkhano umene Mzimu Woyera umabwera nkumadzayendapo. Tawawonani atumiki awa apa, iwo—iwo amakhala kuzungulira mdziko lino kuno, ndipo iwo a... (Zikomo inu, mlongo.) Iwo a—iwo adzakhala okondwa kukhala nanu mu mpingo wawo.

¹⁷⁶ Tsopano ine ndikufuna kuti ndinene ichi, kuti munthu aliyense amene watembenuka sabata ino, munthu aliyense amene watembenuka kuno sabata ino, tsopano, ayang'ane pa gulu ili la atumiki, iwo—iwo akuimirira chinthu chomwecho chimene ine ndikuchiimirira. Ife tiribe kutsutsana kumodzi nkomwe. Ndife ndithudi ofanana. Ife timakhulupirira mu Uthenga wathunthu, ubatizo wa Mzimu Woyera, zinthu zonse izi. Atumiki onse awa pano, ife tonse ndi ofanana ndendende chimodzimodzi. Ndipo ife tikufuna kuti inu mukajowine tchalitchi chawo kuti inu muzipitirizabe. Tsopano iwo ali... Msamariya wabwino wabwerapo, wadzatsanulira mafuta mu bala. Koma iye wakutangani inu tsopano, ndipo iye akufuna inu kuti mupite ku imodzi ya nyumba za alendo kuno, yapafupi ndi inu. Iye wawalipira kale abusa kuti akusamalireni inu, chotero iye walipira; iye analandira Mzimu Woyera, analandira madalitso a Mulungu, ndi thanzi, ndi vumbulutso, iye akhoza kungodyetsa solo yanu! Chotero inu mubwere tsopano ndipo mudzajowine chimodzi cha matchalitchi awo, ndipo icho chi—icho chidzakhala chinthu chapamwamba chimene inu mungadzapange kuti mudyetse mzimu wanu ndi kumayendabe. Mulungu akhale nanu.

¹⁷⁷ Tsopano, ife sitimadzinenera kuti ndife chirichonse choposa m'bale wanu. Tsopano, ngati Mkwatulo ungabwere lero, ndipo Mulungu nkuwatengera kaye kwawo oyenera awokoyamba, ine ndingakhale womalizira kuchoka pa nsanja. Uko nkulondola. Ine ndinabadwa kunjwa kwa nyengo. Ine... Pamene inu, ambiri a atumiki a Pentekoste inu pano, achikulire kuposa ine, zaka zapitazo munali kunjwa kuno pa msewu, mukulalikirira, pamene kunali kuzunzika kochuluka, inu munali kupaza njira imene ine ndikuthamangamo. Inu munkawauza anthu kuti zinthu izi zikanadzachitika. Inu munkayenera kudula mitundu yonse ya tchire ndi zinthu, kudutsa mtundu uliwonse wa mulu wa miyala. Mukuona? Ine ndangokhala mwana basi. Ndipo inu ndi amenewo, inu ndi abale amene—amene mwabweretsa ichi. Ndinu abale ndi alongo amene mwachita zinthu izi. Inu munkangoyankhula izo kwa anthu, ndipo munkawauza iwo kuti izo zikanadzabwera. Inu munkakaika maziko. Mmodzi ndi... amaika maziko, wina ndi kalipentara, wina ndi pulambala, wina ndi wazamagetsi. Nyumba ya Mulungu ikumangidwa.

Mukuona? Ndipo tsopano pamene ife tikupitirira, ndipo aliyense ali ndi malo ake. Ndipo tsopano ife—ife tikufuna kuti anthu inu muziwalemekeza ndi kupereka ulemu kwa abale athu ndi mipingo iyi. Ndi kulola Ufumu wa Mulungu ukule ndi kuwonjezereka mowirikiza, ndiro pemphero lathu.

¹⁷⁸ Tsopano, ine sindingathe kuchiritsa. Machiritso anagulidwa kale ndi Mzimu Woyera. Ndi angati akudziwa zimenezo? Khristu anachita zimenezo pa Kalvare. Chinthu chokhacho, chimene mwinamwake amuna awa apa, iwo ndi atumiki, iwo akhoza kutenga Mawu a Mulungu. Ine sindingathe. . . Ine sindingayerekeze kuima patsogolo pawo ndi Mawu a Mulungu, ndi chirichonse chotsutsana; chifukwa, iwo ndi oitanidwa, imeneyo ndi ofesi yawo, iwo amalalikira, iwo amadziwa chimene iwo akuchinena. Chotero ine ndimangomvetsera kwa chimene iwo akunena, ndikuti “ameni” ndi kumapitirira, chifukwa iwo ali—iwo ndi amuna a Mulungu. Ine ndimawatsatira iwo, ndipo ine ndimapenza kuti iwo ali mu Baibulo, ndipo akunena Choonadi.

¹⁷⁹ Chabwino, tsopano, ine si wakuti ndizilalikira. Koma mphatso yanga ndi mphatso ya kupenya. Ndiyo a. . . Yesu anali mlaliki. Iye analinso mpenyi. Ndipo mbali yanga, pokhala kuti ine ndiribe maphunziro okwanira kuti ndizilalikira, koma ine ndiri ndi mphatso yopenyeratu zinthu, ndimaneneratu ndi kulosera.

¹⁸⁰ Pakuti, mu Baibulo, Ilo linati, “Anatumizidwa atumwi, aneneri, avangeri, aphunzitsi, abusa, onsewa kwa ungwiro wa Mpingo.” Mulungu anawaika iwo mu Mpingo. Tsopano, ziripo mphatso zauzimu naini, zimene ife tikhoza kusanjikapo manja, ndi zina zotero, ndi kupemphera moona mtima kufuna mphatso zabwino, ndi kumawonetsera monga choncho. Koma zinazi ndi mphatso zokonzedweratu za Mulungu, Mulungu amaziyika izo mu Mpingo.

¹⁸¹ Kwa m’badwo umene ukubwera, Iye. . . Yohane M’batizi, anali wotsogolera wapadera wa m’badwo umenewo. Mulungu anangomudzozeratu iye kuti akachite ntchito imeneyo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndithudi, Iye anatero. Yesu anati, “Kodi inu munapita kuti mukamuwone mneneri?” Anati, “Woposa mneneri.” Mukuona? Yohane samadziwa zimenezo, koma Yesu ankadziwa izo. Mukuona?

¹⁸² Ndipo Yereimiya, iye asanabadwe, Mulungu anati, “Ine ndinakudziwa iwe, ndinakuyeretsa iwe, ndipo ndinakudzoza iwe udzakhale mneneri ku mafuko.” Izo nzoona, si choncho izo?

¹⁸³ Tsopano pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, pamene Iye anapita kuti azichoka, Iye anati, “Kanthawi pang’ono, ndipo dziko. . .” Musaiwale ichi, mzanga wa Chikhristu. “Kanthawi pang’ono, ndipo dziko silimandiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti

Ine ndidzakhala ndi inu, mwa inu, ngakhale kumathero a dziko.” Kodi Iye ananena zimenezo? Iye akanadzakhala ndi ife mpaka kumapeto a dziko lapansi. Baibulo limanena kuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse.” Zimenezo zikutanthauza, “yemweyo mu kachitidwe, yemweyo mu mphamvu.” Chinthu chokhacho chosiyana mwa Yesu lero pa dziko lapansi, kuposa mmene Iye anali nthawi imeneyo, lero Iye ali pano mmaonekedwe a Mzimu Woyera. Thupi Lake likukhala ku dzanja lamanja la Mulungu Kumwamba. Tsiku lina Iye adzabwera, ndipo iwo amene ali mwa Khristu adzauka ndi kudzapita ndi Iye. Mukuona? Icho ndi chimene ife tikuchiyembekezera, tsiku limenelo. Koma Mzimu Wake, ndi mphamvu Zake zonse ndi kuwonetseredwa, zinaperekedwa ku Thupi la okhulupirira dziko lonse.

¹⁸⁴ Tsopano, Mngelo wa Ambuye uyu: ngati Iye sachita ndi kupanga ntchito zomwezo zimene Yesu ankachita, ndiye Iwo si Mzimu umene unali pa Yesu, koma ngati Iwo *uti* uchite ntchito zomwezo zimene Yesu ankachita! Chifukwa Iye anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita, iyenso adzazichita.”

¹⁸⁵ Inu mukudziwa Baibulo limanena, mutu womwewo, Yohane 14, “Ntchito zimene Ine ndikuchita, iyenso adzazichita; ngakhale *zochuluka* kuposa izi iye adzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate anga.” Ine ndikudziwa King James amanena kuti “zoposa.” Izo sizingakhale zoposa; lapachiyambi limati “zochuluka.” Chifukwa, Iye anaimitsa chirengedwe, Iye anaukitsa akufa, chabwino, basi chirichonse. Iwe sungachite zazikulu kuposa zimene Iye ankachitira. Koma Mpingo udzachita zochuluka za izo, chifukwa, pamene ife tikuchititsa msonkhano pano, iwo akuchititsa msonkhano mu Afrika, iwo akuchititsa iyo ku Brazil, iwo ali kuzungulira dziko lonse, mwaona, chifukwa izo zikuyenera kukhala *zochuluka*. Mulungu anawonetseredwa mwa Munthu mmodzi nthawi imeneyo, Mwana Wake Yesu; tsopano iye akuwonetseredwa mu Mpingo Wake, dziko lonse. Koma Mzimu womwe womwewo ukuchita ntchito zomwezo! Tsiku lina . . .

¹⁸⁶ Kwa inu amene mulibe khadi la pemphero. Tsopano, pali khadi lapemphero limodzi lina mu—mwa omvetsera? Ngati liripo, inu mubwere mu mzere. Inu amene mulibe makadi a pemphero, panali mkazi . . .

¹⁸⁷ Tiyeni tinene—tiyeni tinene izo monga chonchi, izo sizimawerengeka mwanjira iyi, koma mkazi nthawi ina anali ndi vuto la magazi, ndipo iye sankadziwa kuti akafika motani kwa Yesu. Koma iye anati, “Ngati ine ndingagwire mphonje ya chovala Chake, ine ndikumukhulupirira Iye, ine ndikachiritsidwa.” Ndi angati amene anayamba awerengapo nkhani imeneyo? Bwanji, ndithudi, ife tinatero.

¹⁸⁸ Ndipo, tsopano, iye anazembera mu chigulu, ndipo anazembera kudutsa otsutsa onse, ndipo iye anakagwira chovala Chake. Tsopano, chovala cha Chipalestina chimakhala chomasuka, ndipo iwo ankakhala ndi chovala chamkati. Tsopano, Iye sanamverere izo mwa thupi, koma Iye anati, “Ndani wandikhudza Ine?” pamene iye anadzamukhudza Iye nabwerera mwa omvetsera. “Ndani wandikhudza Ine?”

¹⁸⁹ Ndipo, bwanji, Petro anamudzudzula Iye, anati, “Ambuye, Inu munganene bwanji chinthu ngati chimenecho? Bwanji, aliyense akukukhudzani Inu, ndipo Inu mukuti, ‘Ndani wandikhudza Ine?’” Iye anamudzudzula Iye, Baibulo limatero.

¹⁹⁰ Iye anati, “Koma Ine ndazindikira kuti Ine ndafooka, ukoma wachoka mwa Ine.” Ndipo Iye anayang’ana paliponse mwa omvetsera mpaka Iye anamupeza mkazi wamng’onoyo. Ndipo Iye anati kwa iye, “Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe.” Iye anali ndi vuto la magazi. Mukukumbukira zimenezo? Tsopano, ndi angati . . .

¹⁹¹ Penyani, akulu a mpingo awa apa, nonsenu ndi azibusa. Abale okhala abusa, Baibulo linanena kuti “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Nkulondola uko? Ndipo Baibulo limanena kuti “Iye ndi Wansembe Wamkulu, akukhala ku dzanja lamanja la Mulungu tsopano, akupanga chitetezero pa zodzinenera zathu.” Iye ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudziwa ndi kumverera kwa zofooka zathu. Nkulondola uko? Mukuona zimenezo? Wansembe Wamkulu. Tsopano, ngati Iye ali yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse, kukhudza kofanana kukhoza kubweretsa zotsatira zomwezo. Nkulondola uko?

¹⁹² Tsopano inu muyang’ane kwa Iye. Kodi inu mungamukhudze chotani Iye? Ndi chikhulupiriro chanu. Kufikira kumeneko ndi kuti, “Ambuye Yesu, ine ndiri ndi chosowa chosimidwa.”

¹⁹³ Mvetserani. Pemphani ichi. Musadzipempherere nokha; mumupempherere winawake. Tiyeni tizitenge izo mwanjira imeneyo. Osati monga inumwini; mumupempherere winawake. Mzimu Woyera uwone zimenezo. Mungomupempherera winawake. Ena a okonedwa anu, kapena winawake amene inu mukudziwa kuti ali kwinakwake, kapena chinachake monga choncho, mupempherere chimenecho. Mwaona, kuti inu mudziwe . . . musati- . . . Iwo sakusowa kuti achite kukhala pano. Mulungu amamva pemphero. Iye amadziwa chimene inu mukuchipempherera.

¹⁹⁴ Ndi angati mnyumba muno ali alendo kwa ine, amene ine sindikudziwa kalikonse ka inu? Kwezani dzanja lanu. Zikomo inu. Ine ndikuganiza, munthu aliyense. Pansi pa mzere wa pemphero uno, aliyense wa inu mukudziwa, inu mukudziwa kuti ndine mlendo kwa inu, kwezani dzanja lanu. Ine sindikukudziwani inu.

¹⁹⁵ Tsopano, inu mukuzindikira, ngati kukhudza kumodzi kuchokera kwa mkazi wamng'ono kunamufooketsa Yesu Khristu Mwana wa Mulungu, ukoma unachoka mwa Iye (*ukoma* ndi “mphamvu”), mzere umenewo ungachite chiyani kwa ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo? Mwaona, ndi kumeneko kutanthauzira kwanu, “*Zochulukwa* kuposa izi inu mudzazichita.” Mukuona? Ndi zimenezotu. Tsopano, ngati ine ndingatenge theka la mzere wa pemphero umenewo, pa kuzindikira za mumtima, iwo mwinamwake akhoza kundinyamula ine. Izo zimangondifooketsa ine. Pamakhala chinachake chokhudza izo. Ine sindingachite zonsezo. Koma ine ndikhoza kumupempherera aliyense. Zimenezo ndi zimene inu mukufuna, mulimonse, si choncho anthunu?

¹⁹⁶ Kuikana manja. Tsopano, Yesu, Iye sanati, “Mudzaika manja ndi kupemphera.” Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira, ngati iwo adzayika manja pa odwala.” Sanati nkomwe “adzawapempherera iwo”; basi “adzaika manja pa iwo.” Dongosolo lopemphera ndiro, “Kuitana akulu a mpingo, kuwalola iwo awadzoze iwo mmafuta ndi kuwapempherera iwo,” zimenezo ndi za mpingo. Koma mphatso ya uvangeri ya machiritso imangokhala “kuyika manja pa odwala.” Ife tikudziwa zimenezo. Osati “kuwapempherera iwo”; “Kuyika manja pa iwo, zizindikiro izi zidzawatsatira!” Tsopano, koma kuti a . . .

¹⁹⁷ Tiyeni tiwone, uyu ndi . . . M'bale Borders, ndani? Chabwino. Basi kuti Mzimu Woyera uyambe, ndi kumayenda pakati pathu.

¹⁹⁸ Tsopano, taonani, ine sindikufuna kuti aliyense aziyendayenda. Chonde, tsopano, paliponse, mukhale chete kwenikweni, mukhale molemekeza. Tsopano, ine ndikutanthauza, pamene Mzimu Woyera uchita chirichonse, inu mukufuna kumupembedza Iye, izo nzabwino, inu muzichita zimenezo. Koma musayendeyende. Mungokhala chete. Chifukwa, aliyense wa inu ndi mzimu. Ndiyeno kudzoza kwa Mzimu Woyera kukabwera ndi, kuti, winawake kumbuyo uko akuti, “Ine ndikudabwa ngati zimenezo ziri zooni,” ine ndikuzimverera izo pano. Winawake kumbuyo uko akuti, “Kuti, John, kodi iwe ukumudziwa *Wakuti ndi wakuti* ndi *Wakuti ndi wakuti*. Ine ndinali *wakuti ndi wakuti*.” Mwaona, zimenezo zimasokoneza.

¹⁹⁹ Mwaona, chifukwa, ngati Mzimu waukulu wa Moyo Wamuyaya uli ndi ife, ndipo Iwo wandidzodza ine kwa chinachake, ndiye ine ndimachimverera icho basi monga kugunda kwa mtima. Mwaona, inu . . . Umo ndi mmene ine—ine ndimazipezera izo. Mwaona, inu mukamukhudza Iye. Ndipo kudzera mu zimenezo, pamene inu mupemphera kwa Iye, chikondi chanu ndi chikhulupiriro zimamakukhudza Iye; zikatero Iye basi . . . ine ndimangodzipereka ndekha, ndikatero

Iye amayankhula, ndipo amayamba kundiuza ine. Ndiye inu mukhala woweruza ngati izo ziri zoonza kapena ayi.

²⁰⁰ Tsopano ngati Iye angachite izi kwa nthawi yomaliza, tsopano ife tikuchoka, tikukonzekera kutero, msonkhano ukukonzekera kuti utsekedwe mu maminiti pang'ono otsatirawa, ndi angati amene angati, “ine ndivomereza izo ndi mtima wanga wonse, ndi kukhulupirira chirichonse chimene ine ndikuchisowa”? Mulungu akudalitseni inu tsopano.

²⁰¹ Atate Akumwamba, mmanja Mwanu ine ndikupereka omvetsera awa. Ine ndikutenga mzimu uliwonse pano pansu pa ulamuliro wanga, kwa ulemu ndi ulemelero wa Yesu Khristu. Ine ndikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

²⁰² Tsopano, dona apa, ine ndikukhulupirira (anangokwezera mmwamba dzanja lake) kuti iye ndi mlendo kwathunthu kwa ine. Ine sindikumudziwa iye. Mwinamwake nthawi yathu yoyamba imene ife tinakhalapo moyandikana chomwechi, pokhapokha ngati tinadutsana penapake pa msewu kwinakwake. Koma Mulungu akutidziwa awiri tonsefe. Tsopano ngati...

²⁰³ Tsopano penyani, amzanga. Pano pali chithunzi lero cha Yohane Woyera 4, mkazi ndi mwamuna kukumana kwa nthawi yawo yoyamba; Yesu ndi mkazi waku Samariya. Tsopano, sindine Yesu, komanso iye si mkazi waku Samariya, koma uno ndi m'badwo wina. Mzimu Wake womwewo uli pano. Mkaziyu wayima apa, iye akhoza kukhala wotsutsa, iye akhoza kukhala Mkhristu, iye akhoza kukhala wonyengezera, iye akhoza kukhala kuti akufuna zachuma, iye akhoza kukhala kuti akumuimirira winawake. Ine sindikudziwa. Ine basi sindingakuuzeni inu. Koma Mulungu akudziwa. Tsopano ngati Iye angaime ndi kudzandiuza ine, ndipo (mumulole iye akhale woweruza) ngati Iye ati andiye ine, ndendende, chinachake chokhudza iye! Ngati ine...pali chinachake chokhudza iye, ine sindingachidziwe icho. Koma ngati Iye angandiye ine chinachake chokhudza iye, mulole iyeyo akhale woweruza wake.

²⁰⁴ Ndiye, chabwino, ngati izo ziri zoonza, inu mukudziwa kuti izo zikuyenera kuti zikubwera kuchokera ku mphamvu inayake. Kodi nkulondola uko? Ina...Chabwino, ndiye inu mungaidziwe bwanji Mphamvu imeneyo? Ndiyo kulalikirira Uthenga, kumukweza Yesu Khristu, kuitanira ochimwa ku guwa, kuchiritsa odwala ndi osautsika, ndi mtundu wanji wa Mzimu, ndi mtundu wanji wa zipatso umene Mzimu umenewo ungabereke? Mtundu womwewo wa zipatso zimene Yesu Khristu ankabereka, ndi Mzimu wa Mulungu pa Iye. Nkulondola uko? Iwo udzakhala Mzimu wa Chikhristu. Chifukwa, zidzakhala kwa inu kuti mupange chisankho, ndi uti.

205 Koma izo zingakhale Mulungu kwa inu, si choncho izo? [Mkazi akuti, “Inde, izo zikhoza kukhala”—Mkonzi]. Inde. Chifukwa, iye ndi Mkhristu.

206 Tsopano, ine ndadziwa bwanji kuti iye ndi Mkhristu? Chifukwa ine ndikumverera Mzimu wake, mwaona, pompano, basi monga kugunda kwa mtima kukubwera, monga kumati, psyi, psyi, psyi. Ndipo ine ndikudziwa Mzimu wa Mulungu umene uli pa ine, umene ukundidzozo ine tsopano, ukuzindikira kuti ameneyo ndi mlongo wanga. Ndipo ine sindinamuonepo iye, komabe ine ndikudziwa kuti iye ali. Mwaona, ndi basi chinachake chikubwera monga *chonchi*. Izo zikuyendera limodzi. Mzimu wake ukugwirizana ndi Mzimu umene wandidzodza ine.

207 Ndi angati amene anachiwonapo chithunzi cha Mngelo uja wa Ambuye? Iwo ali, oh, iwo ali nazo izo kuno paliponse, izo ziri pa dziko lonse. Kumbukirani, ine ndikumuzani inu ichi. Mngelo uja wa Ambuye amene inu mumamuwona pa chithunzi, Lawi la Moto limene linawatsogolera ana a Israeli, limene linadasanduka thupi ndi kudzakhala pakati pathu, linachokera kwa Mulungu ndipo linapita kwa Mulungu, labwereranso mmasiku otsiriza kudzachita ntchito yake, kudzamalizitsa Ufumu, liri pomwe pano mkati mwa ma inchesi sikisi ndi pamene ine ndaima. Tsopano mukumbukire zimenezo. Ndi chitsutso bwanji! Koma ine ndikumukhulupirira Iye. Iye amadziwa. Ine ndikudziwa kuti Iye samalephera konse.

Tsopano ngati Ambuye angawulule kwa ine chinachake chokhudza inu, mlongo.

208 Ndipo kwa inu mu mzere wa pemphero, tsopano mungokhala okonzeka, chifukwa ine sindikufuna kuti ndiimire pa kuzindikira za mu mtima nkomwe, chifukwa izo... Ine sindingachite izo. Koma inu mungokhala okonzeka, mukhale mukukhulupirira.

209 Tsopano, ngati ine ndingathe kukuthandizani inu, ndipo osachita izo, ndiye ine ndikhoza kukhala woyipa, ine sindikuyenera kuyima pano pa guwa ili; ndipo nkukhala munthu woteroyo, ndithudi ayi. Koma ine ndakhala ndikulalikira mwamphamvu. Ndipo ine ndikungodikirira kamphindi, kuti ndilankhulane nanu.

210 Chimodzimodzi monga Ambuye wathu anachitira kwa mkazi pa chitsime, Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Mukuona? Kodi Iye anali kuchita chiyani? Amagwira mzimu wake, kuwona limene—limene linali vuto. Ndiye pamene Iye anadzapeza vuto lake, Iye anamuuzza iye chimene vuto lake linali. Inu mukukumbukira chimene ilo linali? Iye anali ndi amuna faifi; ndi sikisi, iwo anali, chifukwa iye anali ndi faifi ndipo amene ankakhala naye nthawi imeneyo anali wa sikisi.

211 Ndipo—ndipo pamene Iye anamuza iye kumene vuto lake linali, bwanji, iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri.”

212 Mwaona, a—a—Afarisi anali atangonena kuti, “Iye anali wambwebwe, mdierekezi.” Iye anawauza iwo kuti izo zikhoza kukhululukidwa. Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera, kudzachita izo, izo sizidzakhululukidwa, kudzayankhula motsutsa Iwo.

213 Chotero, koma iye anati, “Ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri. Ndipo ife tikudziwa (ife Asamariya, ife timawadziwa Mawu), ife tikudziwa pamene Mesiya adzabwera, Amene akutchedwa Khristu, Iye adzatiuza ife zinthu zonse izi.” Mwaona, iye anadziwa kuti chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya.

Ndipo Iye anati, “Ine ndi Iye amene akuyankhula ndi iwe.”

214 Ndipo iye anasiya mtsuko wa madziwo, ndipo anathamangira mu mzinda, ndipo anati, “Bwerani, mudzawone Mwamuna Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndachita. Kodi uyu si Mesiyo?”

215 Tsopano, ngati chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya nthawi imeneyo, icho chikhoza kukhala chizindikiro cha Mesiya pano, ngati Mesiya ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ngati Mzimu uwu umene . . .

216 Inu mukudziwa, kuti chinachake chikuchitika, sichoncho inu? Tsopano mungowadziwitsa omvetsera. Kumverera kokoma kwenikweni, kodzichepetsa kwakhala kukuchitika, kuli pa inu. Si kulondola kumeneko? [Mkaziyo akuti, “Izo nzoona”—Mkonzi]. Kwezani dzanja lanu. Mokoma kwenikweni, modzichepetsa. Ine ndikuwona Kuwala pakati pa ine ndi mkaziyo. Tsopano iko kukuchokapo.

217 Mkaziyo akuvutika ndi TB. [Mkaziyo akuti, “Inu mukulondola”—Mkonzi]. Ndipo iye wangobwera kumene kuchokera ku chipatala cha chifuwa chachikulu. [“Oh, oh, oh!”] Izo nzoona. [“Kulondola”] Pali munthu winanso. Ndi mnyamata uyu apa. Miniti chabe. Mzimu womwewo uli pa iye. Chabwino, ameneyo ndi mdzukululu wanu wamwamuna. [“Inde, ndi choncho. Kulondola.”] Uko nkulondola. Iye ali ndi vuto la kutsekeka mmphuno. Iye alinso ndi minofu yovulazidwa pa mapapo ake. Izo nzoona. [“Uko nkulondola. Ndendende kulondola.”] Uko nkulondola, si choncho? [“Uko nkulondola. Izo ziri. Madkotala ananena kuti iye ali nazo.”] Ndithudi. Chabwino. Akazi a Harris, ndiro dzina lanu. [“Ndiro dzina langa!”] Inu ndi mdzukululu wanu wamwamuna kazipitani kwanu, mavuto anu atha. Yesu Khristu wakupangani inu . . . ? . . .

218 Inu mukumukhulupirira Ambuye Yesu tsopano? Mwaona, limenelo ndiro Baibulo, umenewo ndi Mzimu wa Mulungu

ukuchita zomwezo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Tsopano kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Izo zikuyenera kukhazikitsa izo.

²¹⁹ Tsopano ngati ine sindinena liwu limodzi, kudzangoika manja anga pa inu pamene Kudzoza kuli pano, kodi inu mungakhulupirire? Kazipitani ndiye, ndipo mukachiritsidwe, mu Dzina la Yesu Khristu.

²²⁰ Bwerani, mlongo. Inu mukufuna kuthana ndi vuto lanu la mmimba? Kazipitani, mukuthokoza Mulungu, ndikuti, “Ilo latha,” mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

²²¹ Ngati ine nditi ndiyike manja anga pa inu, inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Mu Dzina la Yesu, muchiritsidwe. Ndicho chikhalidwe choti ulowemo. Iye anachiritsidwa. Uko nkulondola. Ndiro khalidwe lake. Tsopano, kumbukirani, Mzimu Woyera uli pano.

²²² Apa pakubwera mnyamata wamng’ono wokoma. Ndiwe wamng’ono kwambiri, wokondedwa, zovuta, kuti ungakhale ndi chikhulupiriro. Koma tayang’ana kuno miniti chabe, kwa M’bale Branham. Chabwino. Vuto lako la mtima latha tsopano. Iwe ukhoza kupita kwanu ndipo ukakhala bwino. Amen. Yesu wakuchiritsa iwe.

²²³ Tiyeni tinene, “Zikomo Ambuye,” chifukwa cha mnyamata wamng’ono uyo.

²²⁴ Wakhala wamanjenje kwambiri, sichoncho iwe? Zikusiya iwe tsopano. Uzingopita kwanu, ukunena, “Zikomo inu, Ambuye,” ndipo ukachiritsidwe.

²²⁵ Bwera. Chabwino, nthenda ya shuga yakale ija, ngati ife tingathane nayo iyo! Kodi iwe ukukhulupirira ndi mtima wonse? Mu Dzina la Yesu, mulole iyo imuchokere mkaziyo ndipo isadzamuvutitsenso iye kenanso. Amen.

²²⁶ Bwerani tsopano. Dona uyu anali ndi chinthu chomwecho, nthenda ya shuga, nayenso. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano pamene mukudutsa, ndipo muchiritsidwe, mu Dzina la Ambuye Yesu.

Kodi inu mukukhulupirira, aliyense tsopano? Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu!

²²⁷ Bwerani, mlongo wanga. Mu Dzina la Yesu Khristu, muchiritsidwe. Mukhale ndi chikhulupiriro, musakaikire.

²²⁸ Bwerani, m’bale wokondedwa. Ine ndithudi ndikukhulupirira kuti inu munachiritsidwa pamene inu munakhala pansu apo, chotero inu mukhoza kumangopitirira!...?....Mulungu akudalitseni inu tsopano. Chabwino.

²²⁹ Bwerani, mlongo wokondedwa. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu! Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu. Mu Dzina la

Yesu Khristu, uchiritsidwe. Amen. Mulungu akudalitse iwe, mlongo. Zipitirirani, mukusangalala ndi kukhulupirira. Oh, limenelo ndiro khalidwe lobwera nalo.

²³⁰ Tsopano mungokhala molemekeza kwenikweni, aliyense asunge mpando wake tsopano. Mukhale olemekeza kwenikweni, Mzimu Woyera uli pano. Basi chifukwa choti Iwo sumayankhula mochulukwa kwathunthu kwa iwo; nthawizina umangonena zinthu. Ine ndikungoyesera kuti ndinene... Ndipo ngati ine ndiwona izo zikuwonekera mwachangu, ine ndimanena izo kenako nkumapitirira. Mukuona? Nthawizina ine ndikhoza kubwera pa izo kenanso kwa maminiti angapo, ndipo kenako nkumapitirira. Koma Mzimu Woyera uli pano, Iye akudziwabe zinthu zonse.

²³¹ Inu mukukhulupirira zimenezo, dona? Bwerani kuno miniti. Ndine wotsimikiza, inu pokhala wa Chispanish, ndipo ine Irish, ife sitikudziwana wina ndi mzake. [Donayo akuti, “Ayi”—Mkonzi]. Iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukumana. Inu mukumukhulupirira Yesu Khristu, Uyu amene ine ndikumukambayu, ndi Mwana woona wa Mulungu? Inu mukukhulupirira kuti ine ndikumumirira Iye molondola? Inu mukukhulupirira kuti Iye ananditumiza ine kuti ndidzakuthandizeni inu? [“Inde”] Ngati ine ndikuuzani inu limene liri vuto lanu, inu mumukhulupirira Iye? Vuto lanu liri mu nsana wanu. Inu muli ndi vuto la nsana. Komanso, amuna anu ali ndi vuto la nsana. Iye ali ndi vuto ndi mwendo wake. Inu muli ndi mtsikana amene ali ndi vuto ndi khosi. Izo zinayambira kuchokera pa ngozi ya galimoto. Uko nkulondola. [“Oh, zikomo Inu, Ambuye!”] Pita kunyumba, nonse mukakhala bwino.

²³² Khalani ndi chikhulupiriro. Musakaikire. Tsopano zimenezo zimafooketsa ndipo zimachita chinachake. Mungokhala ndi chikhulupiriro tsopano, mukhulupirire izo.

Mu Dzina la Yesu, ine ndikumupempherera mkaziyu. Amen.

²³³ Bwerani tsopano. Bwerani, bwana. Musakaikire tsopano. Inu mwakhala wamanjenje moyipa ndipo mwagwedezeka, ndipo zakupangitsani inu kukhala ndi zilonda mmimba mwanu, ndipo zikukupwetekani inu. Koma pitani kwanu tsopano, inu mukakhala bwino ndipo mukachira. Mulungu akudalitsemi inu. Mukhale ndi chikhulupiriro tsopano. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

²³⁴ Chabwino, ife tikukhoza kuwona vuto limene liri ndi mwana wamng’ono, iye wavala zothandizira kuyenda apa. Inu mukhulupirira mmalo mwake, mlongo, tsopano, [Mlongo akuti, “Inde, ine ndikutero.”—Mkonzi], kuti Mulungu amulola mtsikana wamng’ono uyo akhale moyo, ndipo akula ndi kudzakhala mzimayi wamng’ono wabwino wopanda zothandizira kuyenda izi?

²³⁵ Okondedwa Atate Akumwamba, ngati ine ndikanatha kumuchiritsa mwana uyu ndikuchotsa zothandizira kuyenda izi pa iye, ine ndikanachita izo. Koma ine ndikuyika dzanja langa pa mwana wamng'ono wokondedwa uyu, amene alibe njira yokhalira ndi chikhulupiriro payekha. Ine ndikudzudzula chikhaliidwe cholumala ichi. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mwana uyu ayende ndipo akakhale moyo. Basi motsimikiza basi monga mmene ine ndaimira pano. [Mlongo akuti, "Iye wachiritsidwa"—Mkonzi]. Ndithudi. Inde. Inu mukukhulupirira zimenezo, sichoncho inu? ["Ine ndikutero"] Ndi angati akukhulupirira zimenezo? Iye apita, ndipo mwanayo akachotsa zothandizira kuyendazo, ndipo iye akayenda. Chabwino, khalani ndi chikhulupiriro.

²³⁶ Manjenje a mmimba. Ndipo, oh, mai! Iwe ukukhulupirira? Ndiye zipita, ndipo ukadye ndipo ukakhale ndi nthawi yabwino, ndipo chikhulupiriro chako chakupanga iwe kukhala wamphumphu.

Mukhale ndi chikhulupiriro tsopano, aliyense, mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu! Bwerani, mlongo wokondedwa. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse?

²³⁷ O Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye. Iye akuyenera kukhala ndi mphamvu Yanu yochiritsa, kapena afa. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse iye. Perekani izi. Perekani izi.

²³⁸ Chabwino, mlongo. Ndiloleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Pali anthu ambiri kunja uko mwa omvetsera awa, akuvutika ndi chinthu chomwecho chimene chikukuvutani inu. Mwaona, ndiloleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Inu muli ndi mtima wamanjenje. Ndiloleni ine ndikuwonetseni inu kunja uko. Onse amene akusautsika ndi mitsempha (kwezani mmwamba manja anu) ndi mtima, kwezani manja anu. Tayang'anani pa iwo, mwaona. Ine ndingathe bwanji kumuitana aliyense wa iwo? Mukuona? Ine sindingakwanitse kuchita zimenezo. Koma ine ndikhoza kungomverera kukhudza kwakukulu uko; mdani akuyesetsa kuti akugwireni inu, ndipo akuitanira chifundo kumeneko. Iye asiya kugwira kwake paliponse. Uko nkulondola. Chotero, kodi inu mukukhulupirira iye akusiyani, kuti iye walephera izo pa inu pompano? [Mlongo akufuula, "Inde."—Mkonzi]. Inu mukumverera mosiyana, sichoncho inu? Inu munachiritsidwa nthawi yomweyo. Pitani panjira yanu, mukusangalala, muziti, "Zikomo Inu."

²³⁹ Bwerani, dona wamng'ono, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse ndipo mukhala bwino. Mu Dzina la Yesu, mlongo wathu achiritsidwe.

²⁴⁰ Mulungu, mudalitseni mnyamata wamng'ono uyu usikuuno. Oh, mai! Iwe ukukhulupirira kuti Yesu akuchiritsa iwe? Chabwino. Mu Dzina la Yesu! Mulungu akudalitse iwe.

241 Chabwino. Kazibwerani tsopano, ndipo mukhulupirire, m'bale. Bwerani, m'bale wanga, wotheadizira. Bwerani, inu, mudzatenge madalitso a Ambuye. Ine ndikuika manja anga pa m'bale wanga, mu Dzina la Yesu. Mulole iye achiritsidwe. Perekani izi.

242 Aliyense akukhulupirira? Mukhale ndi chikhulupiro. Musakaikire. Mungokhulupirira tsopano. Basi chifukwa ife sitikuima ndi munthu aliyense, zimenezo sizikutanthauza... Kungonena...Ine ndikuziwona izo, koma basi ine sindikungofuna masomphenya kuti...Icho ndi chinachake ngati cholumikiza mwa iwe pamene iwe ukuyankhula ndi anthu. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza? Icho chimalumikiza, ndipo kenako ndiwe...Ndi zimenezotu, mwaona, ndiwe...Icho chimakufoola iwe.

243 Mphindi chabe, chinachake chachitika mwa omvetsera. Ngati inu muti mukhulupirire, inu simukasowa kuti akakuchiteni opareshoni chikhodzodzo chimenecho. Inu mwakhudza mphonje ya chovala Chake, mlongo. Kodi iye anakhudza chiyani? Ndiuzeni ine chimene iye anakhudza. Izo ndi zosatheka kuti iye andikhudze ine kuchokera pamenepo. Koma iye anachita zimenezo...Tsopano ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Iye anali atakhala pomwe apo nthawi imeneyo, akupemphera, "Mulungu, muloleni iye anditchale ine." Ngati izo nzoona, ngati ndiro pemphero lanu...Ndi zimenezotu, mwaona. Ndizo ndendende. Inu muchite chimodzimodzi, ndipo muwone ngati izo sichoncho. Mungopanga mofanana. Chabwino.

244 Ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ine sindikukudziwani inu, ndipo inu simukundidziwa ine. Mulungu akutidziwa awiri tonsefe. Pamene Kudzoza kuli pano, ife tingowona kuti vuto lake ndi chiyani. Chinthu choyamba, inu mukuvutika ndi maso anu, mutu wanu. Inu muli ndi mfundo pa nkono wanu wa kumanzere ndi padzanja. [Mkaziyo akuti, "Uko nkulondola"—Mkonzi]. Uko nkulondola. Inu mukukhulupirira? ["Inde"] Ndinu wochokera ku malo otchedwa Sunnyvale. ["Uko nkulondola"] Akazi a White. ["Inde"] Pitani kwanu, mukukondwerera, ndipo mukakhale bwino. Chabwino.

245 Mukhale ndi chikhulupiro mwa Mulungu, mungokhulupirira tsopano, aliyense. Kazibwerani tsopano ndipo mudzakhale...Kodi inu mukukhulupirira? Aliyense akupemphera? Oh, mungokhala pamaso pa Mulungu, mukupemphera!

Bwerani, m'bale. Mu Dzina la Yesu, mukakhale bwino.

246 Bwerani, mlongo wokonedwa. Bwerani, mukukhulupirira ndi zonse zimene ziri mwa inu. O Ambuye, mu Dzina la Yesu, mchiritseni mlongo wanga. Ameni.

247 Bwerani, mlongo wokonedwa, mungokhulupirira chimene Mulungu akuchita, Kukhalapo Kwake. Inu mukudutsa pansu pa mtanda tsopano. Mu Dzina la Yesu, muloleni iye achiritsidwe.

248 Bwerani, mlongo, mukudutsa pansu pa mtanda, mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse. Vuto la nsanalo lichoka, ndipo mukhoza kupita kwanu ndipo mukakhala bwino. Chabwino. Mu Dzina la Yesu Khristu!

249 Bwerani, mlongo wokonedwa. O Ambuye, ine ndikupemphera, pamene iye akudutsa, kuti Inu mumuchiritse iye. Ameni.

250 Bwerani, mlongo. Mukhulupirire tsopano. Atumiki, pempherani. Aliyense apemphere. Bwerani. Mu Dzina la Yesu, mulole iye achiritsidwe. Ameni.

251 Bwerani tsopano, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Mlongo wosauka, iye ali moyipa kwambiri. Inu mukukhulupirira Mulungu akudziwa chimene chakuvutani inu? Inu mukukhulupirira Iye akhoza kundiuza ine? Ndiye vuto lachikazi likusiyani. Pitani kwanu ndipo mukakhale bwino.

252 Bwerani, mukukhulupirira. Chabwino, mlongo wokonedwa, kazibwerani. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mukuganiza munachiritsidwa kamphindi kapitako pamene ife timawapempherera iwo amene anali ndi vuto la mtima kunja uko? Inu mukutero? Zipitirirani, mukakhale bwino, ndipo mukakhulupirire izo ndi mtima wanu wonse.

253 Tiyeni tinene, “Ambuye alemekezeke,” aliyense. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

254 Bwerani, m’bale wanga. Mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole iye achiritsidwe. Ameni.

255 Si zodabwitsa zimenezo? Kodi Iye si wodabwitsa? Nzosadabwitsa Iye ankatchedwa “Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha”!

256 Mupempherere okonedwa anu. Mungowapempherera (osati nokha) okonedwa anu kwa kamphindi. Mumupempherere winawake.

257 Dona, inu mukukhulupirira? Inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine chimene inu mwayimira pamenepo? Ine ndawona inu muli a . . . Oh, ndinu mmodzi wa ogwira ntchito? Ine sindikukudziwani inu. Ine—ine ndikuganiza sindinakuwonenipo inu osatinso kunja uko mwa omvetsera. Nkulondola kumeneko? Kuti omvetsera adziwe. Uko nkulondola. Inu mukukhulupirira kuti Khristu akhoza kuulula kwa ine chimene vuto lanu liri? [Dona akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndipo ngati Iye atero, ndiye. . . Inde, pokhala kuti iye wavala cholembedwa chimenecho, munthu wina akhoza kukhala muno ndikuti, “Chabwino, ndithudi, iye ndi wogwira ntchito, iye amamudziwa iye.” Ine sindinayambe ndakumanapo nanu mmoyo mwanga,

ine sindikudziwa kalikonse. Koma ngati ine nditakuuzani inu pamene vuto lanu liri, ndi chinachake, inu mukudziwa icho chikuyenera kukhala chinachake pambali pa ine chikuchita izo. Nkulondola uko? [“Uko nkulondola”] Inu simunabwere pano chifukwa cha inueni. [“Ayi”] Inu muli pano chifukwa cha mwana wanu wamwamuna. Uko nkulondola. Ndipo iye ali ndi chinachake cholakwika ndi minyewa yanu. Izo zikukhala ngati ndi kuvunda kwa minyewa. Izo zinamupangitsa iye kupita mu vutolo, maso ake apingasa, ndi chirichonse, wamanjenje kwenikweni. Dzina lake ndi Donald. [“Inde!”] Pitani kunyumba, ndipo mukhulupirire, mulole iye akhale bwino. Mutenge mpango uwo...?...

²⁵⁸ Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Musakaike ayi. Mungabwere, mlongo. Bwerani, mukukhulupirira. Tsopano tiyeni tipemphere, aliyense akhale mu pemphero. Bwerani, mlongo. Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mlongo wanga achiritsidwe.

²⁵⁹ Bwerani tsopano, mlongo wokonedwa. Uko nkulondola, bwerani pafupi. O Ambuye, pamene iye akudutsa pansi pa mtanda wa Khristu, mulole Magazi akhudze thupi lake.

²⁶⁰ Bwerani, mlongo wanga wokonedwa, mukhulupirire mmalo mwa mwanayo. Ndipo, Ambuye, pamene iwo azidutsa pansi pa mtanda, ine ndikuyika manja anga pa iwo ndipo ndikupempha machiritso awo, mu Dzina la Yesu.

²⁶¹ Bwerani, m'bale wanga, mudutse pansi pa mtanda, mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse. Inu mukhoza kulandira chimene mukuchipempha. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Amen.

²⁶² Bwerani, m'bale, chimodzimodzi, pitani pansi kumene pa mtanda, mukukhulupirira. Mu Dzina la Yesu Khristu, perekani izi. Uko nkulondola.

²⁶³ Bwerani, mlongo wanga. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Musakaikire ayi. Mukhulupirire. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupempha kuti chopempha chake chiperekedwe. Amen.

²⁶⁴ Pempherani, abale. Aliyense apemphere, paliponse. Chabwino. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mlongo wanga achiritsidwe.

²⁶⁵ Bwerani, mlongo. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Amen. Bwerani, aliyense amene akupemphera, mwamuna wina kunja uko, zipempheranibe.

Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

Bwerani, mlongo. Mukhulupirire tsopano, ndi mtima wanu wonse. Mu Dzina la Yesu, mukhale bwino.

Bwerani, m'bale wanga. Inu mukukhulupirira? Mwamuna wamkulu, wamphamvu, komabe, muli ndi vuto la mmimba. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndipo muzipita kwanu, mukakhale bwino mu Dzina la Ambuye Yesu. Chabwino, bwana.

Inu mukukhulupirira, mlongo wamng'ono? Chabwino, bwerani kwa ine pano. Mu Dzina la Ambuye Yesu mulole chopempha chake chiperekedwe.

Mukhulupirire, m'bale wanga, ndi zonse zimene ziri mwa inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole chopempha chanu chiperekedwe. Musakaikire; zipitani, inu mukhoza kuwona...?...Bwerani.

Mulungu akudalitseni inu. Zikomo inu bwana...?...Izo ziri bwino, si choncho?

Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Mulungu akudalitseni inu, mnyamata. Mu Dzina la Yesu ukhale bwino.

Bwerani, mlongo. Kodi awa ndi mapeto a makadi a pemphero? Makadi onse a pemphero atha? Inu muli bwanji? Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Inu mukutero. Inu mukhulupirire ndiye kuti Iye akhoza kundiuza ine zonse za vuto lanu lonse? Chabwino. Tsopano, ine ndikukhulupirira inu mwangonena kumene kuti mwatuluka ku chipatala. Chimodzi cha zinthu zimene zikukuvutani inu, inu muli ndi chiuno cholumala, muli vuto mu chiuno chanu. Koma zokuchitikirani zanu za ku chipatala zinali opareshoni ya chikazi; iyo siinachirebe. Uko nkulondola, sichoncho izo? Ndipo dzina lanu ndi Akazi a Potts. Inu pitani kwanu ndipo mukakhala bwino tsopano...?...

²⁶⁶ Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Khalani ndi chikhulupiriro. Bambo uyo wakhala kumbuyo uko ndi amene ine ndikumuwonawona. Iye akupemphera...Iye wavala malaya oyera, otsegula pa kolala, akumupempherera mzake amene wakhala mbali ina ya iye pamenepo ali ndi vuto la mu ubongo. Kodi inu mukukhulupirira, bwana? Imirirani pamapazi anu ndipo mukumereze izo. Muyike manja anu pa mzanuyo pamenepo. Ndi zimenezotu. Mulungu akudalitseni inu. Pitani kwanu ndipo ukakhale bwino, mwana. Yesu Khristu wakuchiza iwe. Aleluya. Iye amamupempherera mzake. Icho ndi chimene chimachita izo. Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu amachita zinthu zimenezi, amakuchiritsani inu. Inu mukukhulupirira zimenezo?

Apa pali mkazi wakhala pomwe apa ali ndi chinthu choyera chaching'ono pa mutu pake, wakhala moyandikana ndi mtsikana yemwe ali ndi chinthu chowoneka cha buluu mu tsitsi lake. Mkaziyo akumupempherera mwamuna wake. Uko nkulondola. Iye anali ndi khansa, ndipo inu mukuopa kuti iyo ikubwereranso pa iye. Uko nkulondola, si choncho?

Chabwino. Inu mukukhulupirira? Imirirani pamapazi anu ndiye, muvomereze Izo. Mu Dzina la Yesu Khristu, iyo imusiye iye.

²⁶⁷ Mupempherereni winawake. Mupempherereni mzanu. Mupempherereni winawake. Apa, kumbuyo uko, ine ndikuwona bambo wakhala kumbuyo kuseri kwa mkazi uyu apa, kumbuyo kwenikweni ndithu, wakhala, wachiwiri wakhala pamenepo, iye akumupempherera mkazi wake. Iye ali ndi vuto la manjenje. Inu mukukhulupirira, bwana? Chabwino, imirirani pa mapazi anu ndipo muvomereze machiritso, ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Pitani kwanu ndipo mukampeze iye akupemphera bwino. Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga wokondedwa. Mukhulupirire ndi zonse zimene ziri mwa inu.

Aliyense winanso akukhulupirira? Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Apa, mtsikana wamng'ono anakweza dzanja lake pomwe apa. Pali Kuwala kukulendewera pa iye. Oh, iye a . . . Apa pali wamng'ono . . . Alipo awiri a iwo. Dona wamng'onoyo anakweza dzanja lake. Dona wamng'ono wakhala moyandikana ndi iye, zikuwoneka ngati Kuwala kukulendewera pa dona wamng'onoyo yemwe wavala diresi lowoneka la buluu. Inu mukupempherera winawake: mphwanu, ali ndi vuto la mtima, manjenje. Uko nkulondola, si choncho? Iye sali pano. Iye ali ku Los Angeles. Ameneyo ndi mchemwali wanu, nchifukwa chake izo zayandikana kwambiri. Iye akupemphera nayenso, koma ndi za mzake. Iye akupempherera kutembenuka kwa mzake uyu. Mzake uyu ndi wa Katolika, ndipo iye akumupempherera iye. Uko nkulondola. Ndinu awiri nonse azichemwali. Ngati izo nzoona, imirirani pa mapazi anu. Mulungu akudalitseni inu. Ine sindikukudziwani inu, sindinakuwoneni inu mmoyo mwanga. Pali chinachake chachirendo chokhudza inu ndiponso. Inu mwinauwake munakhalapo kwinauwake, kapena—kapena mukumudziwa winawake wochokera kwinauwake kumene ine ndinafikako. Ine ndikuwona malo owoneka mwachirendo. Iwo si—iwo sali nkomwe . . . Ndi Germany. Kodi ndinu wa chi German? Uko nkulondola. Inu muli. Izo ndi ndendende kulondola. Chabwino, chikhulupiriro chanu chakupatsani inu chopempha chanu. Pitani kwanu. Inu mukazipeza izo mmene inu mwakhulupirira izo. Aleluya.

²⁶⁸ Ine ndikukubetcherani inu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti mukhulupirire Izo kukhala zoonza. Ine ndi . . . Motani . . . Kodi alipo wochimwa pano amene angafune kubwera pano ndi kudzaima ife tisanapite patsogolo ndi mzere wamachiritso? Mzanga wochimwa, inu amene munabwerera mmbuyo, kodi inu mungakonde mutawadziwa Ambuye Yesu ngati Mpulumutsi wanu wanu? Bwerani kuno miniti chabe pamene limba lizitiimbira ife yoitanira paguwa yabwino yaying'ono. Bwerani kuno. Mzimu Woyera ukudziwa yemwe inu muli. Ngati inu mukumufuna Khristu pompano mmoyo mwanu, kodi

mungatsikire kuno pa nthawi ino ndi kudzaima pano pa guwa? Ino ikhoza kukhala nthawi yotsiriza imene ine ndingapemphere ndi inu mmasiku onse a miyoyo yathu. Uwu ndi mwayi wanu. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata wamng'ono.

Kodi inu mungabwere? Wina wakenso? Bambo akubwera apayu. Wina wakenso? Bwerani mpaka mmusi kuseri kwa sikilini uko, ndipo mubwere mpaka ku guwa tsopano, pamene ife tikudikirira mphindi chabe. Ife tidikirira. Bwerani komwe kuno, bwana, ndipo mudzaima apa.

Wina wakenso akufuna kubwera kudzaima pambali pa iye? Sunthirani mmbuyo. Bwerani mu mtunda muno tsopano ndipo mudzaima apa, kuti ife tithe kukupempherani inu. Ine ndikhala wokondwera. Ine ndikhala wokondwera kwambiri kuti ndipemphere nanu inu. Ingobwerani. Ndizo zonse ife tikukufunsani inu kuti muchite.

Mulungu akudalitseni inu, bwana, dzaimeni pomwe apa. Kodi aliponso wina?

²⁶⁹ Kuli kasupe wodzazidwa ndi Magazi wotengedwa kuchokera mmisempha ya Emmanuele, kumene ochimwa akagwetsedwera pansu mu kusefukirako amataya mabanga a machimo awo. Kodi Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake? Mulungu amakhala mu Mawu Ake? Mulungu amakhala mwa Mwana Wake? Tsopano, kodi Mulungu akukhala mwa anthu Ake? Chabwino, Mulungu ali pomwe pano ndiye. Iye akufuna kuti abwere mwa inu. Kodi inu simubwera?

Kasupe ali wodzazidwa ndi magazi,
Otengedwa...?...

Ataya mabanga a zolakwa zawo zonse.

Kodi mungabwere tsopano, inu amene muli ndi chosowa cha Khristu? Ife sitikusamala kuti inu ndi a tchalitchi chiti, kapena ndi chiti chimene inu mumapitako, kapena ndi chiti chimene inu mutapite. Bwerani. Uko nkulondola. Sunthirani kumtunda kuno kuzungulira guwa tsopano. Inu amene mulibe Mzimu Woyera, kodi inu mungafune kuti mubwere? Bwerani tsopano pamene ife tikuyimba. Kazibwerani.

Momwe ochimwa amadziponyera pansu pa
kusefukirako,
Ataya zonse...

Mulungu akudalitseni inu, wokondedwa. Ine ndiri ndi Sarah wamng'ono kunyumba pafupifupi usinkhu wako. Mwaona izo, amayi?

Ataya mabanga a zolakwa zonse.

Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Kodi inu mwakhutitsidwa kuti Khristu ali mwa anthu Ake? Bwerani

patsoḡolo tsoḡano, inu simuḡero? Ziyendani mukubwera. Dzerani mbali iyi.

Momwe ochimwa amadziponyera pansi pa
kusefukirako,
Ataya mabanga a zolakwa zonse.
Mbala pa kufa anakondwa pakuwona
Kasupe uja mu tsiku lake; (Khristu
waperekedwa kwa inu, mzanga. Kodi inu
mungabwere ndi kudzamulandira Iye?)

...kuti ine, ngakhale (Mulungu akudalitseni
inu. Izo nzabwino. Yendani pomwe...)
Nditsuke tchimo langa lonse.
Nditsuke tchimo langa onse,
Nditsuke machimo anga onse;
Ndipo apo mulole ine, ngakhale woyipa monga
iye,
Nditsuke machimo anga onse.

²⁷⁰ Chotero kuti ine ndikhale wotsimikiza kuti sipadzakhala manja amagazi pa tsiku la chiweruzo akundibaibisa ine ndikuti, “Iwe ukanapitiriza motalikitsa pang’ono,” ine ndikufunsa ndipo ndikuitanira munthu aliyense amene alibe Khristu, wopanda chiyembekezo, wopanda Mzimu Woyera, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukuitanani inu pano pa guwa ili. Bwerani ndipo mumulandire Iye tsoḡano. Koma ngati inu simuḡero, ndiye ine sindidzakhala woyankhira pa tsiku la chiweruzo. Ziganizireni izo tsoḡano, pamene Khristu ali pakati pathu. Ife tikudziwa zimenezo.

Mulungu amakhala mu chirengedwe Chake. Inu mukumuwona Iye kunja uko. Mulungu amakhala mu Mawu Ake. Inu mukumuwona Iye pano. Mulungu akukhala mwa Mwana Wake. Inu mukumuwona Iye pa mtanda. Mulungu akukhala mwa anthu Ake. Inu mukuziwa izo pano zikuyenda, zikugwira ntchito. Izo ziri pano tsoḡano.

Tiyeni tizibwera pamene ife tikuyimba kamodzinso, “Pali Kasupe wodzadzidwa ndi Magazi.” Kodi inu simubwera?

Pali kasupe wodzadzidwa ndi Magazi,
(Kasupeyo ndi uyu. Apa pa mtanda. Kodi
inu simubwera?)
...mmitsempha ya Emmanuele,
Momwe ochimwa amadziponyera pansi pa
kusefukirako,
Ataya mabanga a zolakwa zonse. (Mulungu
akudalitseni inu.)
...mabanga a zolakwa zonse,

Ataya mabanga a zolakwa zonse;
 Momwe ochimwa amadziponyera pansu pa
 kusefukirako,
 Ataya mabanga a zolakwa zonse.

²⁷¹ Kazibweranibe. Uko nkulondola. Zisunthanibe. Ife tikhala tikudikirirabe. Ife tiri ndi nthawi yochuluka yoti tiwadikirire anthu olapa awa kuti abwere pa guwa. Kazibweranibe. Ndife okondwa, osangalala, othokoza kwa Mulungu kuti inu mukubwera. Zisunthani chokwera tsopano mu Kukhalapo kwa Mzimu Woyera, Iye Amene ali wopezeka ponseponse, wamphamvuzonse, wopanda malire. Kodi inu mungabwere tsopano kwa Iye pamene chisomo Chake chikuyendera mokwanira kuti chitipulumutse tonsefe, kuti chikupatseni inu chirichonse chimene inu mukuchisowa. Iye ali pano kuti akupatseni inu Mzimu Woyera, kuti apulumutse moyo wanu, akuchizeni ku nthenda iliyonse, akuchitireni inu chirichonse chimene inu mukuchifuna. Ambuye akudalitseni.

²⁷² Tsopano, pamene omvetsera akupemphera, mwakachetechete, ine ndiyankhula ndi awa amene ali pano. Azimzanga, Chinachake chakuuzani inu kuti mubwere pa guwa ili. Anali Mmodzi yemwe uja amene amadziwa mtima wanu, Mmodzi yemweyo amene akuyankhula apa, Mzimu Woyera, Mulungu. Mulungu ndi Mzimu Woyera mwa anthu Ake, akuyanjanitsa dziko kwa Iyemwini.

Tsopano, Iye wabwera kuti adzakuyanjanitseni inu kwa Iyemwini. Odala ndinu. Odala ndi maso amene atseguka kuti awone Ufumu wa Mulungu. Analipo masauzande ambiri a anthu anu mmbuyo mwanu, mahandiredi ndi mahandiredi a azigogo anu, amene ankafuna kuti adzawone masiku awa. Amuna aakulu ambiri mmbuyo mwathu, amuna ambiri a pambuyo panu ankafuna kuti adzawone nthawi imene Mzimu Woyera ukanadzabwera mu tchalitchi ndi kudzapanga zimene inu mwaziwona zikuchitika masana ano. Iwo anafera mu chikhulupiriro, akukhulupirira kuti tsiku lina ana awo adzawona izo.

Tsopano, inu mwaziwona izo masana ano. Inu mwamva Mawu. Inu mukudziwa kuti Iwo ndi choonadi. Ndipo Mulungu watsegula maso anu; mapemphero awo.

²⁷³ Apa pali atsikana aang'ono ayima apa, mayi ayima, agwirizira atsikana aang'ono awiri. Aang'onowo abwera, akulira. Ine ndikudabwa ngati mwana, ana, nthawi zina samawadzudzula aakulu, kuchokera mu mtima wawo waung'ono wanthete. Iwo sanadutsitse izo kudutsa mmitundu yonse ya zokhumudwitsa za mdziko ndi zinthu. Iwo ndi a nthete ndi okoma. Ine ndikuwaona atsikana aang'ono awiri awa anamukumbatira donayo, basi ngati kuti iwo amayang'anira kuti chinachake chichitike. Ndithudi, Mulungu amayankhula

kwa ana Ake aang’ono. Baibulo linanena chomwecho. “Lolani ana aang’ono abwere kwa Ine. Musawakanize iwo ayi.”

Ine ndikuwona mayi wamng’ono apa wanyamula mwana wake, mwana wamng’ono wokoma, wamunyamula iye mmanja mwake. Iye wabwera apa tsopano kuti adzayanjanitsidwe ndi Khristu. Tsopano, wodala ndi inu. “Palibe munthu angadze kwa Ine . . .”

Mnyamata wagwira mkazi wachichepere, ine ndikuganiza, wayima pamenepo wamugwira iye. Iye akulira. Iye waweramitsa mutu wake molemekeza. Kodi inu mukudziwa kuti ndizo ntchito za Mzimu Woyera? Ena, mtsikana wamng’ono wa maso a bulauni akundiayang’ana ine wapafupifupi usinkhu wa zaka seveni kapena eyiti, maso aang’ono a bulauni ndi tsitsi la bulauni, nkhope yake yonse yaying’ono ndi yowala. Iye akuyembekezera chinachake. Iye akhoza kukhala wachi Spanish.

²⁷⁴ Ine ndikuwona mkazi wamng’ono wokondeka, basi ali pa mphambano ya moyo waweramitsa mutu wake molemekeza, atapinda manja ake. Ine ndikuwaona ena, a tsitsi la imvi, mitu yawo ataweramitsa. Iyi ndi nthawi yopatulika.

Kumbukirani, abwenzi, ife sitinangobwera apa kuti tizingobwera. Ife tabwera chifukwa Mulungu anakuitanani inu. Ndinu zikho za msonkhano uno masana uno. Moonamtima, ndinu zikho za chisomo cha Yesu Khristu, kuti Iye wakuitanani inu kuti mudzayanjanitsidwe ndi kubwera kuti mudzamulandire Iye masana uno. Mulungu akhale nanu.

“Odala ndi iwo (Mukuona?) amene amachita njala ndi ludzu la chilungamo. Iwo adzakhutitsidwa.” Inu mukazipeza zimenezo mu Chiphunzitso cha pa phiri. Yesu ananena chomwecho.

Anyamata ayima pano, basi anyamata, mwinamwake usinkhu wa zaka eyitini, twente, mwinamwake adzakhala alaliki, ine ndingadziwe bwanji? Mwinamwake kuchokera pamenepo adzapita a mishonare amene ati adzawalitse dziko lapansi. Mwinamwake kuchokera mwa anyamata amenewo mudzatuluka mphatso zimene ziti zidzakokere zikwi za miyoyo kwa Khristu, ndipo inu munalipo tsiku limene iwo anabwera ku guwa. Ndi nthawi yopambana bwanji.

²⁷⁵ Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, pamene ine ndikupereka pemphero. “Palibe munthu amene angadze kwa Ine,” anatero Yesu, “pokhapokha Atate Anga atamuitana iye poyamba. Ndipo onse amene adza kwa Ine, Ine sindidzawataya mwanjira iliyonse. Bwerani kwa Ine nonse inu olema ndi othodwa. Ine ndidzakupatsani inu mpumulo.”

Ambuye, ndi awa apa. Iwo abwera chifukwa Inu mwawaitana iwo kuti abwere. Mzimu Woyera mu mtima mwawo wasuntha ndipo wawaitana iwo, ndipo iwo abwera. Apa iwo ayima paguwa, olapa, mitu yoweramitsidwa, akufuna

kuti adzadzidwe ndi Mzimu Wanu wa Wanu—ubwino Wanu. Adzazeni iwo, Ambuye. Moyeretse miyoyo yawo. Atumizeni iwo ku minda kukakolola, anthu awa ayima apa akudikirira. Izo zikhoza kungokhala kunyumba. Izo zikhoza kukhala kutsidya kwa nyanja. Izo zikhoza kukhala kwinakwake, koma zokolola ziripo zakonzeka kuti zikololedwe.

Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu moyeretse miyoyo yawo, ndipo muwadzaze iwo ndi Mzimu, kufikira kuti adzakhale zida zosankhidwa za Inu: mwinamwake mkazi wapakhomo wamng’ono kuti akakolole oyandikana nawo, mwinamwake mwana wamng’ono kuti akayankhule za Yesu kwa mtsikana wamng’ono ku sukulu, mwinamwake anyamata achichepere kuti akatengere Uthenga kupita ku Mexico, dziko lina lachirendo kwinakwake. Perekani izi, Ambuye. Okalamba kuti akayankhule pa ngodya ya msewu kwa mzake, mwinamwake kwinakwakenso: mwamuna wa mfakitore kwa abwana ake, kapena kwa iwo amene ali mu fakitore... Inu mukudziwa, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu muwadzadze iwo pompano, ndi ubwino Wanu ndi chifundo.

Iwo abwera; ine ndikudziwa Inu mwawalandira iwo, chifukwa Inu munati, “Iye amene adza kwa Ine, Ine mwanjira iliyonse sindidzamutaya iye. Iye amene adzandivomereza Ine pamaso pa anthu, iye ine ndidzamuvomereza pamaso pa Atate Anga, ndi Angelo ojera.” Chotero, iwo ayimirira pano pagulu kuti apange kuvomereza: iwo amalakwitsa. Iwo akufuna kukonzeka. Inu muwalandire iwo, Atate. Ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo, ndipo muwapange iwo akhale ana Anu kuyambira ora lino mpakana, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

²⁷⁶ Mulungu akudalitseni inu, mmodzi aliyense wa inu. Mulandire Mzimu Woyera. Tsopano, mupite mchipinda kumene ife tikhoza kukakumana nanu kumbuyo uko, ndi kukayika manja pa aliyense wa inu, kuti tipemphere. Kumbuyo kuno, sunthirani mmbuyo. Kuli chipinda chimene chaperekedwa kumbuyo uko, kumene inu mukakhaleko kwa mphindi pang’ono kumbuyo uko kwa a—kudzadzidwa kwathunthu. Mukagwade pansii; kumuthokoza Mulungu chifukwa chokupulumutsani inu. Mukayikidwe manja pa inu kumbuyo uko pa chosowa chanu, ndi chifukwa cha Mzimu Woyera. Mulungu akudalitseni inu. Adalitse mayi wamng’ono uyu, onse a iwo amene akupita nawo atanyamula ana awo, ndi abambo amene akupalasa tsitsi la mwana wawo wamng’ono, akudziwa kuti iye nayenso akudziwa kuti tsiku lina iye akhoza kudzamuza wamng’ono wake, ife tinakhala mu msonkhano umenewo umene anabwera kwa Ambuye Yesu. (*Bwinoli Tipita.*)

Kuli dziko labwino loposa tsiku,
Mwachikhulupiriro tikuliwona patali.

Pakuti Atate akudikira panjira,
Kutikonzera ife malo komweko.
Bwinoli tipita,
Oh, tikomana pa gombe lokongolalo.
Bwinoli tipita . . .



TIYENI TIMUWONE MULUNGU CHA59-1129
(Let Us See God)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Novembala 29, 1959, ku Santa Clara County Fairgrounds mu San Jose, California, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org